



# Buku la Mphunzitsi

Nthawiyabaibulo  
Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri

Maphunziro A7 - A12



# Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

## Cholinga cha Utumiki

Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

## Masomphenya a Utumiki

Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

## ZOYENERA KUDZIWA

### Zomwe a Bible Educational Services amachita

A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a “Nthawiyabaibulo”, “Moyo Watsopano” ndi “Okolola” a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – [www.besweb.com](http://www.besweb.com) kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

## Keyala

### International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)

Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA

Phone: 00 44 286 632 2462

Email: [sam@besweb.com](mailto:sam@besweb.com)

### UK Secretary – Editorial feedback

Mr Stephen Gillham

Email: [stephen.gillham@besweb.com](mailto:stephen.gillham@besweb.com)

**Web address:** [www.besweb.com](http://www.besweb.com)

**Email address:** [info@besweb.com](mailto:info@besweb.com)

## BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi 0, 1 ndi 2.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa [stephen.gillham@besweb.com](mailto:stephen.gillham@besweb.com).

## KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalsano akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayeseke kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera tayeke kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: **ITALICS**.
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira kotero kuti adzadziwa mavesi ambiri.
- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena

padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.

- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheke yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku [www.freebibleimages.org](http://www.freebibleimages.org) (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

## Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M'buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.

1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

“Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,  
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,  
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa.”

## Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

	KALASI 0 (sanayambe sukulu) Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7) Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10)	Kalasi Yachitatu (Zaka 11-13)	Kalasi Yachinayi (Zaka 14+)
MAPHUNZIRO A	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Chilengedwe</li> <li>2. Nowa</li> <li>3. Petulo</li> <li>4. Petulo - Mtanda</li> <li>5. Abrahamu</li> <li>6. Abrahamu</li> <li>7. Petulo</li> <li>8. Petulo</li> <li>9. Yakobo</li> <li>10. Akhristu Oyambirira</li> <li>11. Paulo</li> <li>12. Nkhani ya Khrisimasi</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Chilengedwe</li> <li>2. Nowa</li> <li>3. Petulo</li> <li>4. Petulo - Mtanda</li> <li>5. Petulo</li> <li>6. Abrahamu</li> <li>7. Yakobo</li> <li>8. Pemphero</li> <li>9. Paulo</li> <li>10. Paulo</li> <li>11. Paulo</li> <li>12. Nkhani ya Khrisimasi</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Chilengedwe ndi Kugwa</li> <li>2. Zochitika Zoyamba - Genesis</li> <li>3. Petulo</li> <li>4. Petulo - Mtanda</li> <li>5. Petulo</li> <li>6. Abrahamu</li> <li>7. Yakobo</li> <li>8. Moyo wa Chikhristu</li> <li>9. Paulo</li> <li>10. Paulo</li> <li>11. Paulo</li> <li>12. Nkhani ya Khrisimasi</li> </ol>
MAPHUNZIRO B	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Moyo Woyambirira wa Khristu</li> <li>2. Zodabwitsa</li> <li>3. Betaniya</li> <li>4. Mtanda</li> <li>5. Mafanizo</li> <li>6. Yosefe</li> <li>7. Yosefe</li> <li>8. Anthu Ankumana ndi Yesu</li> <li>9. Mose</li> <li>10. Mose</li> <li>11. Mose</li> <li>12. Nkhani ya Khrisimasi</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mafanizo</li> <li>2. Zodabwitsa</li> <li>3. Betaniya</li> <li>4. Mtanda</li> <li>5. Akhristu Oyambirira</li> <li>6. Yosefe</li> <li>7. Yosefe</li> <li>8. Alembi a Uthenga Wabwino</li> <li>9. Mose</li> <li>10. Mose</li> <li>11. Mose</li> <li>12. Nkhani ya Khrisimasi</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Mafanizo</li> <li>2. Zodabwitsa</li> <li>3. Betaniya</li> <li>4. Mtanda</li> <li>5. Akhristu Oyambirira</li> <li>6. Yakobo ndi Banja Lake</li> <li>7. Yosefe</li> <li>8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita</li> <li>9. Mose</li> <li>10. Mose</li> <li>11. Lamulo</li> <li>12. Nkhani ya Khrisimasi</li> </ol>
MAPHUNZIRO C	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Danieli</li> <li>2. Zodabwitsa Zina Zambiri</li> <li>3. Anthu Ankumana ndi Yesu</li> <li>4. Imfa ya Khristu</li> <li>5. Rute ndi Samuele</li> <li>6. Davide</li> <li>7. Davide</li> <li>8. Yoswa</li> <li>9. Eliya</li> <li>10. Elisa</li> <li>11. Yona</li> <li>12. Nkhani ya Khrisimasi</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Danieli</li> <li>2. Anthu Ankumana ndi Yesu</li> <li>3. Zodabwitsa Zina Zambiri</li> <li>4. Imfa ya Khristu</li> <li>5. Rute</li> <li>6. Samuele</li> <li>7. Davide</li> <li>8. Yoswa</li> <li>9. Eliya</li> <li>10. Elisa</li> <li>11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale</li> <li>12. Nkhani ya Khrisimasi</li> </ol>	<ol style="list-style-type: none"> <li>1. Danieli</li> <li>2. Zoyankhula za Yesu</li> <li>3. Mphamvu za Ambuye</li> <li>4. Imfa ya Khristu</li> <li>5. Rute</li> <li>6. Samuele</li> <li>7. Davide</li> <li>8. Yoswa</li> <li>9. Eliya</li> <li>10. Elisa</li> <li>11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale</li> <li>12. Nkhani ya Khrisimasi</li> </ol>

## A7 Nkhani Yoyamba

Petulo awuza anthu za Yesu – Iyi ndi nkhani ya kubwera kwa Mzimu Woyera.

	<p><b>Ife tikuphuzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Kunali kofunika kuti ophuzira alandire Mzimu Woyera.</li><li>• Mzimu Woyera amakhala mwa aliyense amene wakhululupirira Ambuye Yesu kukhala Mpulumutsi.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 2:1-14; 36-39</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 2:36</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Gwiritsani ntchito mafunsowa pofotokoza za Mzimu Woyera. Kodi mungathe kuona mphepo? Ayi! Mumadziwa bwanji kuti kuli mphepo? Inu mumaona zomwe imachita. Ngati mungathe kuyang'ana kunja, onani ngati mphepo ikuwomba.</li><li>• Kumbutsani ana nkhani ya Paska - Yesu anafa ndipo anauka kwa akufa. Iye asanapite Kumwamba analonjeza ophuzira ake kuti adzawatumizira Mthandizi wapadera kwambiri.</li><li>• Mthandizi ameneyu ndiye Mzimu Woyera amene ankayenera kubwera kudzakhala m'kati mwawo. Monga mphepo, iwo sadzatha kuona Mzimu Woyera koma adzadziwa za kusintha kumene Iye adzabweretse m'miyoyo yawo.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Tsiku lina, pasanathe nthawi yayitali, Yesu atapita Kumwamba, ophuzira anali pamodzi m'nyumba mu Yerusalemu. (<i>Machitidwe 2:1-4</i>) Mwadzididzi m'nyumbamo munamveka phokoso la mphepo yamphamvu. Kenaka zinthu zooneka ngati malawi amoto zinakhala pa mutu pa munthu aliyense. Kumeneku kunali kubwera kwa Mzimu Woyera! <i>Kodi mukuganiza kuti atumwiwo anamva bwanji m'mitima mwawo, popeza tsopano mphatso yapadera ija yabwera? (anakondwa, anadabwa, anasangalala kuti lonjezo la Yesu lakwaniritsidwa)</i></li><li>• Kenaka anazindikira kuti akuyankhula ziyankhulo zachilendo! <i>Fotokozani kuti nthawi zonse timayankhula chiyankhulo chomwe tinaphuzira kuchokera kwa makolo athu pamene tinali ana aang'ono kapena kuphunzitsidwa. Ophuzira a Yesu sanaphunzitsidwe ziyankhulo zimenezi. Zizindikiro zonsezi zinasonyeza kuti Mzimu Woyera wabwera. Kodi inu mukanadutsa pa nyumbayi nthawi imeneyi mukanaganiza chiyani?</i></li><li>• Anthu amene anali pafupi anamva phokoso limeneli ndipo anadabwa kwambiri. (<i>Machitidwe 2:5-13</i>)</li><li>• Petulo anazindikira kuti iyi inali nthawi yabwino yoti afotokoze zomwe zinkachitika ndi kuwauza za Ambuye Yesu. (<i>Machitidwe 2:36-39</i>) <i>Kambiranani zomwe anayankhula / kufotokoza kwa gulu la anthuwa. (N'zochititsa mantha, kupeza mawu oyenera kuyankhula, kuda nkhwana ndi zomwe anthu angaganize kapena kuchita....) Koma Petulo anatha kuchita izi chifukwa anathandizidwa ndi Mzimu Woyera.</i></li><li>• <i>Anthu amene anamva Petulo akuyankhula ankayenera kupulumutsidwa ku tchimo lawo monga ifenso.</i></li><li>• <i>Fotokozani kuti Mzimu Woyera amaperekedwa kwa aliyense amene wakhulupirira Ambuye Yesu monga Mpulumutsi. Mzimu Woyera adzatithandiza kufotokoza ena za Yesu.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Petulo awuza anthu za Yesu/Petulo alalikira.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <i>Machitidwe 2:36</i>.</p> <p>Awa ndi mawu ena amene Petulo anayankhula pamene ankalalikira. Iye anawauza kuti iwo ndi amene anapha Yesu koma Mulungu anamuukitsa kwa akufa. Izi zikutanthauza kuti Yesu sanali munthu wamba koma Ambuye ndi Mpulumutsi.</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi atumwi anali kuti pamene Mzimu anabwera?</li><li>• Kodi Mzimu anamveka ngati chiyani?</li><li>• Kodi atumwi anaona chiyani?</li><li>• Kodi iwo anatha kuchita chiyani atadzazidwa ndi Mzimu Woyera?</li><li>• Ndani anamva zomwe zinkachitika?</li><li>• Kodi ndi Mtumwi uti amene anayimirira ndi kufotokoza zomwe zinkachitikazo?</li><li>• Kodi Petulo anayankhula za yani?</li><li>• Kodi Petulo anawauza kuti achite chiyani chifukwa cha tchimo lawo?</li><li>• Kodi iwo adzalandira mphatso yanji akachita zimenezi?</li><li>• Kodi Mzimu Woyera amakhala mwa anthu ati lero?</li></ul>

## A7 Nkhani Yachiwiri

**Petulo achiritsa munthu wolumala miyendo - Iyi ndi nkhani ya mphamvu zochiritsa za Mulungu.**

<b>MAWU OYAMBA</b>	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"> <li>• Mphamvu za Yesu zinagwira ntchito kudzera mwa Petulo ndi Yohane pochiritsa munthu wolumala.</li> <li>• Petulo ndi Yohane anafuna kuthandiza munthu wolumalayo ndipo ifenso tikuyenera kuthandiza ena.</li> </ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 3:1-12</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Kalasi Yoyamba - Machitidwe 3:6;</i>  <i>Kalasi Yachiwiri - Machitidwe 3:16</i></p>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"> <li>• Fotokozani za munthu wolumala amene sankatha kuyenda mosamala ndipo ankapempha ndalama kuti azigula chakudya kuti akhale ndi moyo.</li> <li>• Onetsani ndondo ziwiri zoyendera, ndipo fotokozani kuti munthu uyu ankachita kunyamulidwa ndi anzake.</li> <li>• Jambulani chithunzi cha munthu amene anali ndi nkhope ya chisoni kuyimira munthu ameeny.</li> </ul> <ul style="list-style-type: none"> <li>• Tsiku lina Petulo ndi Yohane akupita ku Nyumba ya Mulungu, munthu wolumala anawapempha ndalama. (<b>Machitidwe 3:1-5</b>) - <i>Onetsani kuti iwo anayima pamene panali munthuyo.</i></li> <li>• Gwiritsani ntchito mawu a Petulo. “Ine ndiliba siliva kapena golide, koma chimene ndili nacho ndikupatsa. M’dzina la Yesu Khristu wa ku Nazareti, yenda!” (<b>Machitidwe 3:6-7</b>) - <i>Fotokozani kuti siliva ndi golide zimathandiza kwa nthawi yochepa – izi sizikanachiza miyendo ya munthuyo.</i> Petulo anamupatsa munthuyo chinthu china chomwe chinasintha moyo wake kwathunthu.</li> <li>• Petulo anagwira dzanja lake ndi kumuthandiza kuyimirira. Nthawi yomweyo miyendo ndi mapazi za munthuyo zinalimba. Iye anayamba kuyenda ndi kulumphalumpha kwanthawi yoyamba m’moyo wake! Iye anayamika Mulungu ndipo analowa m’Nyumba ya Mulungu pamodzi ndi Petulo ndi Yohane. (<b>Machitidwe 3:8</b>) <i>Onetsani chithunzi cha anthu a nkhope zosangalala chosiyana ndi choyamba chija. Kodi inu mukanaganiza chiyani mutakhala kuti munali mutamuona munthuyu akupempha tsiku ndi tsiku?</i></li> <li>• Aliyense anadabwa ndi zimene zinachitikazi. (<b>Machitidwe 3:9-12</b>)</li> <li>• <i>Ganizirani momwe ife tingatsanzire zochita za Petulo. Yankhulani za kuthandiza anthu ena powachitira zinthu ndiponso mufotokoze kuti chinthu chofunika kwambiri chomwe tingachitire ena ndi kuwafotokozerana nkhani yabwino ya Ambuye Yesu.</i></li> <li>• <i>Monga munthuyu, nafenso tili ndi mavuto m’miyoyo yathu. Mphamvu za Yesu zitha kuchotsa tchimo lathu monga momwe zinamumasulira munthuyu kuti ayambe kuyenda.</i></li> <li>• <i>Ganizirani za zinthu zina zomwe zingachititse ife kuyamika Mulungu.</i></li> </ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Petulo achirista munthu wolumala miyendo.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Kalasi Yoyamba: Machitidwe 3:6; Kalasi Yachiwiri: Machitidwe 3:16.</b></p> <p><i>Ngati n’koyenera, ana anene Vesi Yoloweza pamene akuyenda kapena kulumpha pamalo amodzi.</i></p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"> <li>• Kodi inali nthawi yanji?</li> <li>• Kodi Petulo ndi Yohane ankapita kuti?</li> <li>• Kodi munthuyu anakhala asakuyenda kwa zaka zingati?</li> <li>• Kodi ankakhala pati tsiku ndi tsiku?</li> <li>• Kodi anapempha chiyani kwa Petulo ndi Yohane?</li> <li>• Kodi Petulo anamuchiritsa mu dzina la ndani?</li> <li>• Kodi Petulo anachitanso chiyani kuonjezera pa kuyankhula?</li> <li>• Tchulani zinthu zitatu zomwe munthuyu anatha kuchita.</li> <li>• Kodi atachiritsidwa anapita kuti?</li> <li>• Kodi mphamvu za Yesu zingachite chiyani m’miyoyo yathu?</li> </ul>



## A7 Nkhani Yachitatu

Petulo m'ndende - Iyi ndi nkhani ya momwe Mulungu amathandizira amene amamutumikira.

	<p><b>Ife tikuphuzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>Akhristu oyamba anakumana ndi mavuto kuchokera kwa atsogoleri achipembedzo amene anapachika Ambuye Yesu.</li><li>Iwo amene amakonda Yesu adzafuna kumumvera Iye ngakhale atakumana ndi mavuto otani.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 4:1-22</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Ahebri 13:6</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>Pakuti nkhani iyi ikupitiriza nkhani yoyamba ija, ndi bwino kuti tionenso fundo zina zoyamba zija pano.</li><li>Gwiritsani ntchito chithunzi cha munthu wosangalala ndi wachisoni ngati poyambira.</li><li>Kodi chinachitika ndi chiyani kuti munthuyo ayambe kuyenda? Onetsetsani kuti ana amvetsa kuti zinali mphamvu za Yesu.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>Izi zitatha, Petulo ndi Yohane analalikirira za Ambuye Yesu, amene anauka kwa akufa, ndipo anthu ambiri anakhulupirira. (<i>Machitidwe 4:1-2, 4</i>) Koma anthu amene ankayang'anira Nyumba ya Mulungu anakwiya kwambiri chifukwa Petulo anawuza anthu zakuti Yesu anauka. Nthawi yomweyo anagwira Petulo ndi Yohane ndi kukawayika m'ndende. (<i>Machitidwe 4:3</i>) - <i>Fotokozani kuti iwo ankamva bwanji m'mitima mwawo nthawi imeneyi.</i></li><li>Mmawa wake anawabweretsa pamaso pa akulu abwalo ndi kuwafunsa mafunso. (<i>Machitidwe 4:5-7</i>) - <i>Fotokozani kuti bwalo la milandu ndi gulu la anthu amene amagamula munthu kuti ndi wolakwa kapena wosalakwa.</i></li><li>Nthawi imeneyi Petulo anathandizidwanso ndi Mzimu Woyera kufotokoza zomwe zinachitika kuti munthuyo achiritsidwe. (<i>Machitidwe 4:8-12</i>) Bwalo linavutika kuti ligwirizane zomwe angachite ndi Petulo ndi Yohane! Iwo anadziwa kuti chodabwitsa chachikulu chachitika koma atakambirana, agwirizana zoti awuze Petulo ndi Yohane kuti asayankhulenso za Yesu. (<i>Machitidwe 4:13-19</i>) - <i>Kodi Petulo ndi Yohane anamva bwanji m'mitima mwawo atawuzidwa zimenezi? Kodi iwo amvera zimenezi?</i></li><li>Petulo ndi Yohane anadziwa kuti kunali kosatheka kuti iwo asayankhule za Ambuye Yesu! (<i>Machitidwe 4:20</i>) - <i>Iwo ankamukonda Yesu kwambiri, motero anatsimikiza zomvera Iye. Iwo ankadziwa kuti adzadalira Ambuye kuti adzakhala nawo ngakhale zinthu zitavuta motani. Mzimu Woyera adzawathandiza.</i></li><li>Yesu akufunanso kuti tizimukonda ndi kumumvera ngakhale titakumana ndi zovuta zotani.</li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Petulo m'ndende.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <i>Ahebri 13:6</i>.</p> <p>Mutha kuchita sewero. Lembani mizere ya mawu amene ali mu vesi pa bodi. Kenako ophuzira aganize mawu amene akusowekera. Kodi mukuganiza kuti mawu amenewa akanakhala othandiza kwa Petulo ndi Yohane? Fotokozani kuti kudziwa mawu amenewa kungatithandizenso ife!</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<p>Khalani ndi ziganizo zili m'musimu pa kadi kuti ana aziyankha kuti Zoon/Zabodza. Chiganizo chilichonse chili ndi malikisi ake. (5 mpaka 100). Khalani m'magulu awiri.</p> <ul style="list-style-type: none"><li>Apolisi anakwiya kwambiri chifukwa cha Petulo ndi Yohane.</li><li>Iwo anagona m'ndende usiku umenewo.</li><li>Pamene anatulutsidwa anafunsiidwa m'bwalo la milandu.</li><li>Petulo anawuza bwalo kuti ndi mphamvu ya Yesu yomwe yachiritsa munthuyo.</li><li>Mzimu Woyera anathandiza Petulo ndi Yohane kuti ayankhule m'bwalo la milandu.</li><li>Petulo ndi Yohane anathawa m'bwalo la milandu.</li><li>Bwalo la milandu linagwirizana kuti awuze Petulo ndi Yohane kuti asayankhulenso za Yesu.</li><li>Petulo ndi Yohane anati adzamvera chigamulo cha bwalo la milandu.</li></ul>

## A7 Nkhani Yachinayi

### Petulo amasulidwa - Iyi ndi nkhani ya Mulungu kuyankha pemphero.

	<p><b>Ife tikuphonzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Mulungu amapereka mphamvu ndi thandizo kwa Akhristu kuti agwire ntchito yake.</li><li>• Pemphero ndi lofunika pa nyengo ina iliyonse.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 4:23-31</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 4:31 kapena Mateyu 6:33</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Fotokozani nkhani yomwe mukufuna kuti ana akawuze anzawo kapena abale awo – ikhale nkhani yabwino ya zomwe anachita nthawi imene anapita koyenda kapena za kupambana pa mpikisano wawo. Kapena mwina akhala akudandaula pa chinthu china ndipo akuyenera kuwuzwa anzawo amene awathandize.</p>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Petulo ndi Yohane anali ndi nkhani yoti afotokozere anzawo. <b>(Machitidwe 4:23)</b> <i>Fotokozani kuti nkhani yabwinoyi inali ya kutuluka kwawo m'ndende koma nkhani yoyipa inali yakuti anawaletsa kuyankhulanso za Yesu!</i></li><li>• Anzawo a Petulo ndi Yohane anachita chisankho choyenera kuti apemphere. <b>(Machitidwe 4:24-30)</b> Iwo ankadziwa kuti Mulungu ndiye ankalamulira. Iye anali wamphamvu kuposa anthu amene ankawaletsa aja. Pamene ankapemphera, iwo anakumbukira zinthu zodabwitsa zomwe Mulungu anachita poonetsera mphamvu zake. Iwo anapempha Mulungu kuti wapatsa kulimba mtima kuti achite zodabwitsa mwa mphamvu za Yesu. <b>(Machitidwe 4:29-30)</b></li><li>• Iwo atapemphera, Mulungu anayankha mapemphero awo! <b>(Machitidwe 4:31)</b> <i>Fotokozani kuti nyumbayo inagwedezeka chifukwa Mulungu anaonetsanso mphamvu ya Mzimu Woyera amene ankayenera kumakhala nawo kuwathandiza kuti ayankhule za Ambuye Yesu.</i></li><li>• <i>Fotokozani kuti titha kupemphera kwa Mulungu pamene tikufuna kuchita zinthu zovuta.</i></li><li>• <i>Mulungu amamva ndipo amayankha mapemphero athu ndipo adzatithandiza kuti Yesu akhale woyamba, monga anzathuwa mu nkhani imeneyi.</i></li><li>• <i>Kwa ana a Kalasi Yachiwiri, mutha kuwafotokozera za Akhristu amene akukhala m'mayiko amene amaletsedwa kuwuzwa ena nkhani yabwino ya Yesu. Ife tiwapempherere kuti Mulungu awapatse kulimba mtima kuti ayike Ambuye Yesu kukhala woyamba.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Petulo amasulidwa/Petulo atulutsidwa m'ndende.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Machitidwe 4:31 kapena Mateyu 6:33.</b></p> <p>Pa <b>Mateyu 6:33</b>, mawu akuti “funafunani” akutanthauza kuti muyike mtima wanu pa chimenecho. Ufumu wa Mulungu ukutanthauza chilichonse chimene ndi chofunika pamaso pa Mulungu zomwe ndi kuphatikiza Ambuye Yesu.</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<p>Mafunso anu akhazikike pa nkhani zonse zinayi kuchokera mu A7.</p> <ul style="list-style-type: none"><li>• N'chifukwa chiyani ophonzira a Yesu ankayenera kukhala ndi Mzimu Woyera?</li><li>• Kodi ophonzira anaona chiyani pamene Mzimu anabwera?</li><li>• Tsirizani Vesi Yoloweza: “Yesu amene inu munamupachika, Mulungu wamuyika kukhala Ambuye ndiponso _____.” <b>(Machitidwe 2:36)</b> [Nkhani Yoyamba]</li><li>• N'chifukwa chiyani munthuyu ankapempha ndalama pa Nyumba ya Mulungu?</li><li>• Kodi iye anakhala asakuyenda kwa nthawi yayitali motani?</li><li>• Lembani mawu a mu Vesi Yoloweza amene palibe: “M'dzina la Yesu Khristu wa ku Nazareti, _____.” <b>(Machitidwe 3:6)</b> [Nkhani Yachiwiri]</li><li>• Kodi chodabwitsa ichi chinaonetsa chiyani za Ambuye Yesu?</li><li>• N'chifukwa chiyani Petulo ndi Yohane anayikidwa m'ndende?</li><li>• Kodi bwalo la milandu linawawuzwa kuti asachitenso chiyani?</li><li>• Kodi chinachitika n'chiyani Mulungu atayankha pemphero la anzawo a Petulo ndi Yohane?</li></ul>

## A8 Nkhani Yoyamba

### Petulo athandiza Dorika - Iyi ndi nkhani ya kukhalanso moyo kwa Dorika.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Mphamvu za Ambuye Yesu zinagwira ntchito pochiritsa Dorika.</li><li>• Tikuyenera kuvomereza Ambuye Yesu pa kumukhulupirira.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 9:32-43</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 9:42</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Fotokozani njira zomwe tingathandizire anthu amene ali ndi zosowa pogawana nawo zomwe tili nazo. Ngati n'kotheke gwiritsani ntchito zithunzi zoonetsa zomwe mukugwiritsa ntchito pothandiza ena. chitsanzo: ndalama, chakudya, zovala ndi zina.</li><li>• Fotokozani kuti Dorika anali mayi wachifundo kwambiri amene anakonda Ambuye Yesu. Chifukwa cha ichi, moyo wake onse ankathandiza ena ndipo ankadziwa kusoka ndi kupanga zovala za amene anali osauka.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Tsiku lina Dorika anayamba kudwala kwambiri ndipo anamwalira. (<b>Machitidwe 9:37</b>) - <i>Kodi anzake anamva bwanji m'mitima mwawo?</i></li><li>• Akhristu awiri anapita kukayitana Petulo amene nthawi imeneyi anali ku Yopa. (<b>Machitidwe 9:38-39</b>)</li><li>• Nthawi yomweyo Petulo anafika ku nyumba ya Dorika. (<b>Machitidwe: 9:40-41</b>) - <i>Fotokozani mwatsatanetsatene momwe Petulo anapempherera koyamba, kenaka anayankhula naye, ndipo anagwira dzanja ndi kumuthandiza kuyimirira. Dorika anali ndi moyo! Siyanitsani chisangalalo chinali nthawi imeneyi kusiyana ndi nthawi imene Petulo anali atangofika koyamba. Tsindikani kuti ichi chinali chodabwitsa chimene Petulo anatha kuchita chifukwa cha mphamvu za Ambuye Yesu zomwe zinkagwira ntchito kudzera mwa iye.</i></li><li>• Anthu ambiri anakhulupirira Ambuye Yesu. (<b>Machitidwe 9:42</b>)</li><li>• <i>Ife tikuyenera kukhulupirira Ambuye Yesu monga anthu amene anaona Dorika atakhalanso ndi moyo.</i></li><li>• <i>Fotokozani tanthauzo la zimenezi – ife tikuyenera kuzindikira kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu, Iye ali ndi moyo ndipo ali ndi mphamvu zochotsa machimo athu. Kukhulupirira mwa Yesu zimatanthauza kudalira Iye kwathunthu.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Petulo athandiza Dorika.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Machitidwe 9:42.</b></p> <p><i>Vesi Yoloweza iyi ndi yosavuta ngakhale kwa ana aang'ono – Onetsetsani kuti akuyimvetsa. Onetsetsani kuti mawu akuti “Ambiri” akutanthauza ndani. Kodi chinachititsa kuti akhulupirire Ambuye Yesu ndi chiyani? N'chifukwa chiyani kwa ife kuli kofunika kukhulupirira Ambuye Yesu? Kodi munthu angakhulupirire bwanji Ambuye Yesu?</i></p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi Dorika ankakhala kuti?</li><li>• Kodi ankachita chiyani pothandiza anthu?</li><li>• N'chifukwa chiyani ankathandiza anthu?</li><li>• Kodi anamva bwanji m'mitima mwawo pamene Dorika anamwalira?</li><li>• Kodi ndani anapita kukayitana Petulo?</li><li>• Kodi Petulo anachita chiyani pamene anagwada pamene anagona Dorika?</li><li>• Kodi Petulo anati chiyani kwa Dorika?</li><li>• Kodi Petulo anachita chiyani atayankhula ndi Dorika?</li><li>• Kodi anthu ambiri anachita chiyani ataona kuti Dorika ali moyo?</li><li>• Kodi Vesi Yoloweza ikupezeka pati?</li></ul>

## A8 Nkhani Yachiwiri

### Mulungu aphunzitsa Petulo - Iyi ndi nkhani ya chikondi cha Mulungu pa aliyense.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Petulo anamvera ndi kuchita chimene Mulungu anamuwuzwa kuti achite.</li><li>• Mulungu amakonda aliyense ndipo akufuna kuti aliyense adziwe nkhani yabwino ya Ambuye Yesu.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 10:9-23</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Yohane 3:16</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Yankhulani za momwe anthu ochokera mayiko osiyana amakhalanso osiyana – gwiritsani ntchito zithunzi ngati zilipo.</li><li>• Yankhulani za kusiyana kwa maonekedwe a makungu athu, tsitsi, zovala, ziyankhulo ndi zina zambiri.</li><li>• Mulungu analenga munthu aliyense. Iye akufuna kuti munthu aliyense aphunzire za Iye ndi za Mwana wake Ambuye Yesu.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Petulo akupemphera ku Yopa (lumikizani ndi A8 Nkhani Yoyamba). Mulungu anaphunzitsa Petulo kuti Iye amakonda munthu aliyense. (<b>Machitidwe 10:9-16</b>) - <i>Pano sitifotokoza mwatsatanetsatane za masomphenyawo. Kwa ana a Kalasi Yachiwiri, muwafotokozere kuti nkhani iyi inali yovuta kwambiri kwa Petulo kuti amvetse chifukwa anali Myuda ndipo mpaka nthawi imeneyi, iye ankaganiza kuti ndi Ayuda okha amene anali ofunika pamaso pa Mulungu. Petulo anaphunzira kuti aliyense ndi munthu wofunika kwambiri pamaso pa Mulungu.</i></li><li>• Alendo atatu anafika ndipo anapempha Petulo kuti apite nawo ku nyumba ya Korneliyo.</li><li>• (<b>Machitidwe 10:17-22</b>) - <i>Fotokozani kuti Korneliyo anali msilikali wa udindo wake mu gulu la nkondo a Chiroma amene anali wokonzeka kuphunzira zambiri za Mulungu. Korneliyo anali wosiyana ndi Petulo ndipo Petulo sakanapita kukacheza ndi munthu ngati ameneyu. Fotokozani zomwe zinachititsa kuti Petulo azindikire kuti kunali koyenera kuti iye apite (1) kuchokera pa zomwe Mulungu anamuphunzitsa (2) kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera.</i></li><li>• Petulo anapita ku nyumba ya Korneliyo ku Kaisareya (makilomita 64). (<b>Machitidwe 10:23</b>) - <i>Yesani kufanizira za kutalika kwa ulendo umenewu ndi komwe ana amakudziwa bwino. Mwina anayenda mtunda umenewu tsiku lonse. Tsindikani za kumvera Mulungu kwa Petulo poyenda ulendowu.</i></li><li>• <i>Tsindikani kuti Mulungu akufuna kuti aliyense adziwe kuti Iye amamukonda. Iye anapereka Mwana wake kuti afe pa mtanda ndi cholinga chakuti aliyense akhululukidwe.</i></li><li>• <i>Ngati inu munakhulupirira kale Ambuye Yesu, yambani kuthandiza ena kuti nawonso amudziwe Iye.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Mulungu aphunzitsa Petulo/Petulo aona masomphenya.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Yohane 3:16</b>.</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi Petulo ankakhala ndi ndani?</li><li>• Kodi Petulo ankachita chiyani nthawi ya masana?</li><li>• Kodi Mulungu anafuna Petulo azindikire chiyani pamene anayankhula naye?</li><li>• Kodi ndi anthu angati amene anabwera kudzakumana ndi Petulo?</li><li>• Kodi Petulo ankayenera kupita kwa ndani?</li><li>• Kodi Korneliyo ankagwira ntchito yanji?</li><li>• N’chifukwa chiyani Petulo anapita ku nyumba ya Korneliyo?</li><li>• Kodi Mulungu anaonetsa motani kuti amakonda munthu aliyense pa dziko lapansi?</li></ul> <p><b>Sewero:</b> Gawo limene likufotokoza za kufika kwa alendo ana achite sewero pa Nkhani 3. Anthu akulu achite gawo la alendo ndi Petulo.</p>

## A8 Nkhani Yachitatu

Petulo ndi Korneliyo - Iyi ndi nkhani ya momwe Mulungu anapulumutsira mkulu wa asilikali a Chiroma.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Korneliyo anali munthu woyamba amene sanali Myuda (Amitundu) kukhulupirira Yesu momwe zinachitikiramu.</li><li>• Mulungu ndi wokonzeka kukhululukira machimo a aliyense amene angakhulupirire Iye.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 10:23-48</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 10:43</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Pamene tikupitiriza phunziro la sabata latha, n'kofunika kuti tigwiritse ntchito ena mwa mafunso ochokera mu Nkhani Yachiwiri kuti tikumbutsane.</li><li>• Mukachita zimenezi, mutha kufotokozerana zitsanzo zofunika zomwe zinachitika ku dera lanulo zimene zinachititsa anthu kuti asonkhane kudzamva.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Petulo m'nyumba ya Korneliyo: (<b>Machitidwe 10:24-33</b>) <i>Thandizani ana kuti amvetse zomwe zikuchitika – abale ndi abwenzi adzaza m'nyumba ya Korneliyo ndipo aliyense ali ndi chidwi choti amve zimene Petulo ati ayankhule.</i> Korneliyo anafuna kupereka ulemu wapadera kwa Petulo monga mlendo wolemekezeka motero anawerama pamaso pake! Petulo anawuza Korneliyo kuti ayimirire chifukwa iye anali munthu wamba. Kenaka Korneliyo anafotokoza kuti Mulungu anamuwuzira kuti atumize anthu akayitane Petulo. <i>Fotokozani kuti Mulungu anakonzekeretsa anthu awiriwa kuti akumane!</i></li><li>• Uthenga wa Petulo: (<b>Machitidwe 10:34-43</b>) <i>Fotokozani zomwe Petulo anawauza kuti Mulungu akufuna anthu amitundu yonse amukhulupirire.</i></li><li>• <i>Yankhulani fundo zimene anawauza za Ambuye Yesu – Petulo anafotokoza kuti Iye anachita ntchito zabwino, anachiritsa anthu, anaphedwa ndipo Mulungu anamuukitsa kwa akufa. Petulo anafotokoza kuti tsiku lina Ambuye Yesu adzakhala woweruza koma chofunika kwambiri n'chakuti Iye akukhululukira onse amene akumukhulupirira tsopano.</i></li><li>• Zomwe anachita atamva: (<b>Machitidwe 10:44-48</b>) <i>Mzimu Woyera anathandiza anthu awa kuti amvetsetse zimene Petulo anawafotokozerana. Iwo anakhulupirira Ambuye ndipo machimo awo anakhululukidwa.</i></li><li>• <i>Fotokozani kuti pamene tamva nkhani yabwino ya Ambuye Yesu, tikuyenera kuvomereza monga anachitira anthu awa. Ife tikamukhulupirira machimo athu adzakhululukidwanso.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Petulo ndi Korneliyo.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Machitidwe 10:43.</b></p> <p><i>Fotokozani tanthauzo la mawu akuti “aliyense” ndi “kukhululukidwa”.</i></p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<p>M'malo mokhala ndi mafunso ambiri, ndi chanzeru kujambula nkhope za anthu zambiri kuzungulira Vesi Yoloweza. Mwana aliyense ajambule nkhope yake. Izi zithandiza kulimbikitsa choonadi cha chikondi cha Mulungu chomwe Petulo waphunzira ndipo iwo amvetsetse kuti “aliyense” akuphatikiza iwonso. Njira ina mutha kugwiritsa ntchito zithunzi za anthu ena zomwe mwazidula m'mabuku ngati zilipo.</p> <p><b>Sewero:</b> Mutha kuchita sewero la Nkhani Yachiwiri.</p>

## A8 Nkhani Yachinayi

Petulo apulumutsidwa - Iyi ndi nkhani ya Mulungu kuyankha pemphero.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Anzake a Petulo amupempherera.</li><li>• Kuti Mulungu amasankha kuchita zinthu zodabwitsa poyankha mapemphero athu.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 12:1-19</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Yakobo 5:16</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Yankhulani za kugwiritsa ntchito foni poyankhulana ndi anzathu kapena popempha thandizo kwa munthu wina. Ngati muli ndi foni muwaonetse anawo.</li><li>• Bwerezani nkhani ya pemphero monga kuyankhula ndi Mulungu. Mulungu samatiyankhula ife koma nthawi zonse amatimvetsera. Ali ndi mphamvu za kuyankha mapemphero athu.</li><li>• M'nkhani ya lero gulu la anzake linapempherera chinthu china chofunika kwambiri.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Petulo m'ndende: (<b>Machitidwe 12:1-4</b>) Mfumu Herode inkadana ndi otsatira Yesu. Yakobo anaphedwa. Kanthawi pang'ono anagwira Petulo ndi kumuyika m'ndende. <i>Kumbukirani kuti Petulo nthawi ina analinso m'ndende. (Machitidwe 4:3 - A7 Nkhani Yachitatu)</i></li><li>• Mapemphero a anzake a Petulo: (<b>Machitidwe 12:5</b>) <i>Kambiranani n'chifukwa chiyani kutero chinali choyenera kuchita.</i></li><li>• Kutuluka m'ndende: (<b>Machitidwe 12:6-10</b>) Unali usiku woti mawa Petulo azengedwa mlandu (<i>fotokozani kufunika kwa zotsatira za mlandu umenewu kukanakhala kotani</i>). Petulo anamangiridwa kwa asilikali awiri koma iye anagona tulo. Fotokozani momwe mngelo anapulumutsira Petulo zonse zimene zinachitika iye atatuluka. Petulo ankaganiza kuti akulota.</li><li>• Petulo ku nyumba ya anzake: Petulo atafika mu msewu, anazindikira kuti Mulungu wamupulumutsa. <i>Kodi Petulo ankamva bwanji mu mtima mwake nthawi imeneyi? Nthawi yomweyo anapita ku nyumba ya anzake. (Machitidwe 12:11-17) Fotokozani za Roda amene anayankha kugogoda pa khomo ndi chisangalalo chawo. Kodi iwowa ankayenera kudabwa?</i></li><li>• <i>Kambiranani zinthu zimene tikuyenera kupemphera kwa Mulungu. Mulungu nthawi zonse amamva mapemphero athu ndipo amayankha m'njira imene iye akuona kuti ndi yoyenera.</i></li><li>• <i>Tikuyenera kukumbukira kuyamika ndi kutamanda Mulungu pamene wayankha mapemphero athu.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Petulo apulumutsidwa/Petulo m'ndende (kachiwiri).</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Yakobo 5:16.</b></p> <p>Vesi iyi ikutiwuzwa kuti mapemphero athu atha kusintha zinthu. Mulungu amagwiritsa ntchito mapemphero athu kuti agwire ntchito yake.</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi anayika Petulo m'ndende ndi ndani?</li><li>• Kodi Mfumu Herode anali atapha kale ndani?</li><li>• Kodi Petulo ankachita chiyani pamene Mulungu anatumiza mngelo?</li><li>• N'chifukwa chiyani anzake a Petulo anasonkhana pamodzi?</li><li>• Kodi mngelo anawuzwa Petulo kuti achite chiyani?</li><li>• Kodi Petulo anadutsa bwanji pa chipata cha ndende?</li><li>• Kodi mngelo anayenda ndi Petulo mpaka pati asanamusiye yekha?</li><li>• Kodi iye anapita ku nyumba ya ndani?</li><li>• Kodi amene anadziwa kuti ndi Petulo amene ankagogoda pa khomo ndi ndani?</li><li>• N'chifukwa chiyani Roda sanatsekule chitseko koyamba kaja?</li></ul> <p><b>Sewero:</b> Gawo limene Petulo akuchoka ku ndende, anthu awiri atha kuchita sewero, mwana mmodzi ngati Petulo ndipo wina ngati mngelo. Munthu wamkulu azifotokoza zomwe zikuchitika motsatana ndi zomwe anawo akuchita.</p>

## A9 Nkhani Yoyamba

**Yakobo anamiza m'bale wake - Iyi ndi nkhani ya kukhala wodzikonda.**

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Kukhala wodzikonda ndi kudziyika kukhala woyamba ngakhale zomwe ukuchitazo zikupweteka anthu ena.</li><li>• Monga Yakobo, ifenso titha kukhala wodzikonda ndipo kutero ndi kuchimwira Mulungu.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 25:19-34</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 25:28 kapena Afilipi 2:3</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi ana amapasa mumawadziwa? Kodi amaoneka mofanana? Kodi ali ndi makhalidwe ofanana?</li><li>• Kodi inu munayamba mwamenyanapo ndi abale ndi alongo anu?</li><li>• Kodi kudzikonda ndi chiyani? Kodi mungaganize nthawi imene wina amene mukumudziwa anaonetsa moyo wodzikonda ndipo munapwetekeka?</li><li>• Nkhani iyi ndi abale awiri amene sankagwirizana. Mmodzi mwa iwo ankangoganizira za iye yekha basi ndipo ananamiza m'bale wake.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Isake ndi Rebeka ankayembekezera ana amapasa. Ana amapasa asanabadwe, Mulungu anawuza Rebeka kuti mwana wamkulu adzatumikira mwana wamng'ono. (<i>Genesis 25:19-23</i>)</li><li>• Pamene ana amapasawa anabadwa zinaonekeratu kuti adzakhala osiyana kwambiri. Mwana wamkulu Esau, khungu lake linali ndi bweya, koma m'bale wake Yakobo anali ndi khungu losalala. (<i>Genesis 25:24-26</i>) Iwo anakondanso zinthu zosiyana - Esau anali munthu wosaka nyama pamene Yakobo anakonda kukhala pa khomo. Kholo lililonse linali ndi mwana amene linkamukonda. Isake anakonda Esau, pamene Rebeka anakonda Yakobo. (<i>Genesis 25:27-28</i>) - <i>Funsani ana aganizire za kukhala ndi zinthu zimene amazikonda kwambiri.</i></li><li>• Tsiku lina Yakobo anaphika nyemba. Esau anali kosaka nyama. Thandizani ana amvetse zomwe zikuchitika pamenepa – Esau watopa ndipo ali ndi njala ndipo anamva fungo lokoma la nyemba! Esau akufuna adye nthawi imeneyi! Koma Yakobo ndi wochenjera kwambiri. Nthawi yomweyo, iye akuti angapereke nyembazo ngati Esau atamupatsa udindo wokhala woyamba kubadwa. <i>Fotokozani za udindo wa woyamba kubadwa. Mwana wamwamuna woyamba kubadwa ndiye ankapatsidwa udindo umenewu. Izi zinkatanthauza kuti iye adzakhala mtsogoleri wa banja abambo ake akadzamwalira. Iye ankayenera kulandira magawo awiri a chuma cha abambo ake.</i></li><li>• Esau sanaganize bwino; anali ndi njala kwambiri! Iye analola kupusitsidwa ndi m'bale wake ndi kugulitsa udindo wake wa woyamba kubadwa ndi nyemba. (<i>Genesis 25:29-34</i>) <i>Kambiranani zomwe anachita ana awiri onsewa. Kodi Yakobo analondola pomulanda Esau ukulu wake? Kodi kunali koyenera kuti Esau agulitse udindo wake wa woyamba kubadwa ndi mbale ya nyemba?</i></li><li>• <i>Kodi mukuganiza kuti Mulungu anakondwera ndi Yakobo ndi Esau?</i></li><li>• <i>Nthawi zina, monga Esau ndi Yakobo ife timaganiza za zomwe tikuzifuna basi. Pamene tikudzikonda ndiye kuti tikuchimwira Mulungu.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Yakobo anamiza m'bale wake.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza - <i>Genesis 25:28 kapena Afilipi 2:3.</i>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi anyamata awiriwa m'nkhani yathuyi mayina awo anali ati?</li><li>• Kodi wamkulu anali ndani?</li><li>• Tchulani zinthu ziwiri zomwe zinali zosiyana pa ana amenewa.</li><li>• Kodi udindo wa woyamba kubadwa unali wotani?</li><li>• Mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani Yakobo ankafuna udindo wa woyamba kubadwa?</li><li>• Kodi Yakobo anachita chiyani pofuna kupusitsa Esau?</li><li>• Nanga Yakobo ndi Esau anachimwira Mulungu motani?</li></ul>

## A9 Nkhani Yachiwiri

Yakobo anamiza abambo ake - Iyi ndi nkhani ya momwe Yakobo anapusitsira abambo ndi m'bale wake.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Rebeka ndi Yakobo ankafuna kunamiza Isake.</li><li>• Kuchita chinyengo ndi kuyankhula zonama ndi zolakwika pamaso pa Mulungu.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 27:1-29</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 27:20 kapena Salimo 32:2</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi tanthauzo la kuyankhula zonama ndi chiyani?</li><li>• M'nkhani iyi Yakobo akuyankhula zabodza kwa abambo ake. Bodza lake likuvulaza abambo ake ndi m'bale wake kwambiri.</li><li>• Kodi mungakumbukire nkhani zabodza zimene wina anayankhula ndipo zinavulaza munthu wina?</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Nthawi iyi Isake atakalamba sankona. Iye asanamwalire anafuna kudalitsa mwana wake wamkulu Esau. Iye anapemphe Esau kuti amukonzere chakudya chimene ankachikonda kwambiri. (<b>Genesis 27:1-4</b>) - <i>Fotokozani kuti nthawi imeneyi bambo asanamwalire ankayenera kudalitsa mwana wake wamkulu.</i></li><li>• Rebeka anamva kuti Isake akufuna kudalitsa Esau. Iye ndi Yakobo anagwirizana zonamiza Isake ndi cholinga choti adalitse Yakobo. Choncho Rebeka anaphika chakudya chomwe ankachikonda ndipo kuphimba manja a Yakobo ndi zikopa za mbuzi kuti akhale ndi bweya ngati Esau. (<b>Genesis 27:5-17</b>) - <i>Kumbutsani ana kuti kholo lililonse linali ndi mwana amene linkamukonda. Rebeka anakonda Yakobo pamene Isake anakonda Esau. Aliyense wa iwo ankafuna mwana wake wa pantima alandire madalitso. Perekani chitsanzo cha kukondera m'nyumba zathu kapena ku sukulu zomwe ana angathe kuzindikira kuti ndi zolakwika!</i></li><li>• Yakobo anabweretsa chakudya chomwe Isake ankachikonda. Iye ananamiza Isake ndipo anadzaonetsa ngati anali Esau. Isake anadabwa kuti Esau anafulumira kupeza nyama yomwe ankayikonda ndi kukonza chakudya msanga. (<b>Genesis 27:18-20</b>) <i>Kodi mukuganiza kuti Rebeka ndi Yakobo anakondweretsa Mulungu? Chifukwa chiyani? Ngati si choncho ndi chifukwa chiyani?</i></li><li>• Isake anali wodabwa. Kodi uyu analidi Esau? Iye anafuna kuti atsimikize choncho anamuuzza kuti akufuna kumusisita bweya pa khungu la m'mikono yake. Inde... manja ankaoneka ngati a Esau koma mawu ankamveka ngati a Yakobo. Izi zinasokoneza maganizo a Isake. Motero, Yakobo ananamanso ndipo anawuza abambo ake kuti anali Esau. (<b>Genesis 27:21-24</b>)</li><li>• Isake anadya chakudya chimene Yakobo anabweretsa. Atatsiriza kudya, iye anadalitsa Yakobo, poganiza kuti akudalitsa Esau. (<b>Genesis 27:25-29</b>) <i>Kodi mukuganiza kuti Isake anamva bwanji mu mtima mwake pamene anazindikira kuti anamunamiza?</i></li><li>• <i>N'chifukwa chiyani Mulungu analamula kuti tisamanamizane?</i></li><li>• Ganizani chitsanzo cha Ambuye Yesu amene nthawi zonse ankayankhula zoono.</li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Yakobo anamiza abambo ake.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Genesis 27:20 kapena Salimo 32:2.</b>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi mwana wokondedwa wa Isake anali ndani?</li><li>• Kodi mwana wokondedwa kwa Rebeka anali ndani?</li><li>• Kodi Isake asanamwalire ankafuna kuchita chiyani kwa Esau?</li><li>• Kodi Rebeka ankafuna kuti Esau alandire madalitso? Ngati si choncho, chifukwa chiyani?</li><li>• Kodi Yakobo ndi Rebeka anachita chiyani pofuna kunamiza Isake?</li><li>• N'chifukwa chiyani Isake sanazindikire kuti anali Yakobo?</li><li>• Kodi mukuganiza kuti Yakobo ndi Rebeka anakondweretsa Mulungu m'nkhani imeneyi? Ngati si choncho, chifukwa chiyani?</li></ul>



## A9 Nkhani Yachitatu

### Yakobo akumana ndi Mulungu - Iyi ndi nkhani ya chisamaliro cha Mulungu.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Ife tingathe kudalira Mulungu chifukwa amasunga malonjezo ake nthawi zonse.</li><li>• Mulungu amatisamalira.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 28:1-22</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 28:16 kapena Salimo 86:11</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kumbutsani ana zomwe Yakobo anachita ponamiza Isake mu nkhani yathu ya m'mbuyomu. Esau anakwiya kwambiri ndipo anakonzaka chiwembu chofuna kupha Yakobo. Yakobo anaganiza zochoka kwawo kwa kanthawi.</li><li>• Funsani ana kuti adzitenge okha kukhala ngati Yakobo. Kodi iwo akanamva bwanji mu mtima poona kuti akuchoka kwawo m'njira yotere?</li><li>• Fotokozani kwa ana kuti ngakhale Yakobo anachita zinthu zolakwa, Mulungu ankamusamalabe ndi kumukonda. Nkhani yathu ya lero ndi ya kuti Mulungu aonekera kwa Yakobo.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Isake anadalitsa Yakobo ndipo anamulangiza kuti achoke kwawo ndipo apite kwa amalume ake a Labani ku Harani. Ndipo kumeneko akapeze mkazi wake. (<b>Genesis 28:1-5</b>)</li><li>• Ali pa ulendowu, Yakobo anayima pamalo pena kuti agone usiku umenewo. Iye anatenga mwala ndi kutsamira. <i>Taganizani kutsamira mwala!</i> Ali mtulo, analota makwerero amene ankachokera pansu mpaka kumwamba. Angelo a Mulungu amakwera ndi kumatsika pamenepo. (<b>Genesis 28:10-12</b>)</li><li>• Mulungu anali atayima pamwamba pa makwererowo. Iye anawuza Yakobo kuti adzamudalitsa ndi kumupatsa zidzukululu zambiri. Mulungu analonjeza kukhala ndi Yakobo. Tsiku lina Mulungu adzamubweretsanso Yakobo kwawo. (<b>Genesis 28:13-15</b>) - <i>Kambiranani kuti lonjezo ndi chiyani. Kodi inu mumasunga malonjezo nthawi zonse? Ngati si choncho, chifukwa chiyani? Fotokozerani ana kuti Mulungu amasunga malonjezo ake nthawi zonse. Iye ndi Wamphamvuzonse ndipo sanganame.</i></li><li>• Pamene Yakobo anadzuka anazindikira kuti pa malopo panali Mulungu. <i>Fotokozani za mmene Yakobo anachitira mantha poganiza kuti Mulungu anali naye pa malopo. Yakobo anali atachita zolakwika zambiri zomwe sizinakondweretse Mulungu. Koma Mulungu ankamusamalirabe!</i> Kenaka anatenga mwala umene unali mtsamiro wake ndi kuthirapo mafuta. Iye anawatcha malowo Beteli. Yakobo analonjeza kuti ngati Ambuye angakhale naye pa ulendo wake ndi kubwereranso kwawo, pamenepo Ambuye adzakhala Mulungu wake. (<b>Genesis 28:16-22</b>) Yakobo ankayenera kuphunzira kuti Mulungu amasunga malonjezo ake!</li><li>• <i>Ife tili monga Yakobo chifukwa timachita zolakwika zambiri. Mulungu amatikonda ndipo amasalimalira aliyense wa ife, monga momwe anakondera Yakobo. Fotokozani kuti Iye anatumiza Mwana wake kudzatifera ife pa mtanda. Ambuye Yesu ndi "makwerero" wotifikitsa ife kwa Mulungu, kutifikitsa ife ku nyumba yathu Kumwamba.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Yakobo akumana ndi Mulungu.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Genesis 28:16 kapena Salimo 86:11.</b>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• N'chifukwa chiyani Yakobo anachoka kwawo?</li><li>• Kodi Yakobo anagwiritsa ntchito chiyani ngati mtsamiro?</li><li>• Kodi Yakobo anaona chiyani m'maloto ake?</li><li>• Kodi Mulungu anawuza Yakobo chiyani m'maloto?</li><li>• N'chifukwa chiyani zikuoneka ngati zodabwitsa kuti Mulungu anasalimalira Yakobo?</li><li>• Kodi ife timadziwa bwanji kuti Mulungu amatisamalira?</li><li>• Kodi Yakobo anachita chiyani ndi mwala uja?</li><li>• Kodi Ambuye Yesu ali ngati makwerero motani?</li></ul>

## A9 Nkhani Yachinayi

**Yakobo apeza mkazi - Iyi ndi nkhani ya kunamizidwa kwa Yakobo ndi amalume ake.**

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Yakobo wachinyengo, ananamizidwanso.</li><li>• Ife tichitire anthu ena zomwe tikufuna kuti iwo atichitirensa.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Genesis 29:1-30</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Genesis 29:28 kapena Agalatiya 6:7</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi munapitapo kukakhala ndi banja limene simunalidziwepo n'kale lomwe? Kodi munamva bwanji mu mtima mwanu? Kapena, fotokozani zomwe zinakuchitikirani zofanana ndi nkhanayi. Kumbutsani ana kuti Yakobo ankapita kukakhala ndi amalume ake a Labani ku Harani.</li><li>• Bweretsani anthu ena atsopano m'nkhanayi: Labani ndi ana ake aakazi, Leya ndi Rakele.</li><li>• M'nkhani iyi Yakobo akuzindikira tsopano zomwe munthu amamva akanamizidwa.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Yakobo anali pa ulendo wopita ku Harani. Kumapeto kwa ulendo wake anakumana ndi abusa aziweto pa chitsime. Iwo ankawadziwa amalume ake a Labani. (<b>Genesis 29:1-8</b>)</li><li>• Rakele mwana wamkazi wa Labani anafika pa chitsimecho ndi nkhosha zake. Yakobo anamuthandiza kutunga madzi a nkhosha zake pogubuduza mwala umene unali pamwamba pa chitsimecho. (<b>Genesis 29:9-10</b>)</li><li>• Yakobo anamuwuzira Rakele kuti iye anali yani. Rakele anathamanga ndi kupita ku nyumba kwawo kukawuzira abambo ake Labani amene anayitana Yakobo kuti akhale naye m'nyumba mwawo. (<b>Genesis 29:11-14</b>) - <i>Taganizira zina zomwe iwo anakambirana atakumana!</i></li><li>• Yakobo anayamba kugwira ntchito kwa Labani. Yakobo ankayenera kugwira ntchito zaka zisanu ndi ziwiri kuti akwatire Rakele. Iye anali wokonzeka kuchita izi chifukwa anakonda Rakele. (<b>Genesis 29:15-20</b>)</li><li>• Koma kenaka Labani ananamiza Yakobo. M'malo momupatsa Rakele, iye anamupatsa Leya kukhala mkazi wake. (<b>Genesis 29:21-27</b>) - <i>Kodi mukuganiza kuti Yakobo anamva bwanji mu mtima mwake pamene anazindikira kuti wanamizidwa? Komanso izi zinamukumbutsa zomwe iye anachitira ena. Funsani ana kuti akumbukire zomwe Yakobo anachita.</i></li><li>• Yakobo anakwatiranso Rakele koma anayenera kugwiranso ntchito zaka zina zisanu ndi ziwiri. (<b>Genesis 29:29-30</b>) Apa zikuoneka kuti Labani anamupusitsa Yakobo!</li><li>• <i>Mwina Yakobo anakumbukira ndi kuzindikira momwe iye anavulazira anthu ena pa bodza ndi zachinyengo zomwe anachita. Tsopano tikuona kuti akuphunzira m'njira yopweteka. Patapita zaka zambiri, Yesu anaphunzitsa omutsatira ake njira yabwino. Iye anaphunzitsa kuti ife tikuyenera kuchitira ena zomwe ife tikufuna kuti azitichitira. Miyoyo yathu idzakhala yosangalala ngati tingamvere chiphunzitsa cha Yesu.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera A – Yakobo apeza mkazi.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Genesis 29:28 kapena Agalatiya 6:7.</b>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi Labani ankakhala kuti?</li><li>• Kodi ana aakazi a Labani mayina awo anali ndani?</li><li>• Kodi Yakobo anathandiza Rakele motani pamene anafika ku Harani?</li><li>• Kodi Yakobo anakonda mkazi uti?</li><li>• Kodi Yakobo anali wokonzekera kugwira ntchito kwa zaka zingati kuti amukwatire?</li><li>• Kodi Labani anachita chiyani ponamiza Yakobo?</li><li>• Kodi Yakobo anagwiranso ntchito zaka zina zingati atakwatira Rakele?</li><li>• Kodi Yesu ananena chiyani pa nkhanu ya kuchitira zinthu anthu ena?</li></ul>

## A10 Nkhani Yoyamba

Stefano apyedwa chifukwa cha Yesu - Iyi ndi nkhani ya chikondi chachikulu cha Stefano pa Yesu.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Stefano anakonda Mulungu komanso anakonda adani ake.</li><li>• Yesu anali ndi Stefano pamene ankamupha ndi miyala ndipo ankamudikira Kumwamba.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 6:8-15; 7:54-60</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>1 Yohane 4:19</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Funsani ana za nthawi zimene akhala akuthandizidwa ndi ena.</li><li>• Kodi inu mungamve bwanji mu mtima mwanu ngati mukufuna kuthandiza munthu amene sakufuna kuthandizidwa? Nanga atakuyankhulani za chipongwe kapenanso kufuna kukupwetekani?</li><li>• Nkhani ya lero ikuchokera m'Baibulo ndipo ndi ya munthu amene ankathandiza anthu ena. Tiyeni tione zomwe ena anamuchitira munthu ameneyu.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Stefano anakonda Ambuye Yesu. Iye anachita zinthu zodabwitsa ndi mphamvu ya Mulungu zomwe zinathandiza anthu koma Ayuda ena sankamukonda kapenanso kukonda Yesu. Iwo anaganiza zomukonzera chiwembu ndi cholinga choti aleke kuwuzana anthu zakuti Yesu anawafera. (<b>Machitidwe 6:8-11</b>)</li><li>• Anthu awa anayankhula zabodza zambiri za Stefano ndipo anachititsa anthu ena kuti adane naye. Iwo anabwera naye ku bwalo la milandu kuti aweruzidwe. Iwo analinso ndi mboni zomwe zinayankhula zonama zomwe ankati anayankhula ndi Stefano. (<b>Machitidwe 6:12-15</b>) Kodi inu mukanamva bwanji mu mtima mwanu mukanakhala ndinu Stefano?</li><li>• Ngakhale anthu ankayankhula zonama za Stefano ndi Yesu, Stefano sanapse mtima. Anthu anazindikira kuti iye anali ndi Yesu – akuti nkhope yake inkaoneka ngati ya mngelo. (<b>Machitidwe 6:15</b>) Stefano ankateteza Yesu koma izi zinachititsa kuti anthuwo akwiye kwambiri. (<b>Machitidwe 7:54</b>) M'malo mochita mantha, Stefano anayang'ana Kumwamba ndipo anaona Yesu akumudikira kumeneko. (<b>Machitidwe 7:55-56</b>) Kodi Stefano anamva bwanji mu mtima mwake pamene anaona Yesu?</li><li>• Anthu aja anakwiya kwambiri ndi Stefano ndipo sanafunenso kumva zimene ankayankhula. Iwo anatenga Stefano ndi kupita naye kunja kwa mzinda kumene anamupha ndi miyala. Pamene anakachita izi, Stefano anapemphera kuti Yesu amulandire Kumwamba komanso kuti awakhululukire anthu amene ankamuphawo. Kenaka anamwalira. (<b>Machitidwe 7:57-60</b>)</li><li>• <i>Stefano asanamwalire anapempha Yesu chinthu china pa adani ake - Inu mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani anachita zimenezi?</i></li><li>• <i>Kodi ife tingakhululukidwe bwanji pa zoyipa zomwe timachita?</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Stefano apyedwa chifukwa cha Yesu/Stefano apyedwa chifukwa cha Ambuye.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>1 Yohane 4:19.</b></p> <p>Fotokozani kuti Stefano anakonda Ambuye Yesu ndipo anali wokonzeka kufa chifukwa cha Iye. Ambuye Yesu anali ataonetsa kale chikondi chake pa Stefano pamene anafa pa mtanda.</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Stefano anali mtumiki mu mpingo. Kodi iye ankatumikira motani?</li><li>• Kodi aliyense anakonda Stefano? N'chifukwa chiyani sankamukonda?</li><li>• Kodi Ayuda anachita chiyani kuti anthu ayambe kudana ndi Stefano?</li><li>• Kodi Stefano anachita chiyani pamene anthu anayankhula zabodza za iye ndi Yesu?</li><li>• Kodi Stefano anaona chiyani atayang'ana Kumwamba?</li><li>• Kodi anthu anachita chiyani kwa Stefano?</li><li>• Kodi Stefano anapemphera chiyani?</li><li>• Kodi ife tingakhululukire ena motani?</li></ul>

## A10 Nkhani Yachiwiri

Filipo afalitsa uthenga wabwino - Iyi ndi nkhanu ya munthu wa ku Afrika amene anakukhulupirira Yesu.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Tikuyenera kukhulupirira Ambuye Yesu kuti machimo athu akhululukidwe.</li><li>• Mulungu amatithandiza kuti timvetsetse magawo ovuta a Mawu ake, Baibulo.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 8:26-40</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 8:35</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Funsani ana kuti afotokoze za chipululu. Kodi chimaoneka motani? Kodi mungamve bwanji muli ku chipululu? Ngati inu mutawuzidwa kuti mupite ku chipululu mukayankhule ndi munthu amene simukudziwa, kodi mungapite?</li><li>• Kapena mungakumbukire nthawi imene munakumana ndi chinthu chomwe simunkachimvetsa, chitsanzo: buku, masamu ovuta? Kodi ndi ndani amene anakuthandizani?</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Filipino anakhulupirira Yesu ndipo ankalalikirira nkhanu yabwino ya Yesu m'matauni ndi m'mizinda. Tsiku lina mngelo anamuwuzira kuti apite ku msewu opita ku chipululu. (<i>Kodi Filipino mwina ankaganiza chiyani nthawi imeneyi?</i>) Filipino anaona galeta likubwera kumene kunali iye. Iye anaona kuti munali munthu wofunika kwambiri wa ku Etiopia amene anali pa ulendo wobwerera kwawo. (<i>Fotokozani komwe kuli malo amenewa.</i>) (<b>Machitidwe 8:26-28</b>) Kodi mukuganiza kuti munthu wa ku Etiopia ameneyu ankafuna kumva za yani?</li><li>• Kenaka Mzimu Woyera anawuzira Filipino kuti apite komwe kunali munthuyo. Iye ankawerenga mokweza mawu buku la Yesaya, buku la Chipangano Chakale. Filipino anamufunsa ngati ankamvetsa zomwe ankawerenga, koma munthuyo sankamvetsa! (<b>Machitidwe 8:29-31</b>). Vesi imodzi ya mavesi amene ankawerenga inkanena za munthu wina amene adzaphedwa ngati mwanawankhosa. (<i>Fotokozani kuti nkhusa simavuta akayitenga kupita kukayipha.</i>) Filipino anafotokoza kuti mavesiwo ankayankhula za kufa kwa Ambuye Yesu pa mtanda chifukwa cha machimo athu. (<i>Fotokozani za kudzipereka kwa Yesu kutifera.</i>)</li><li>• Munthu wa ku Etiopiayu anamvetsa kuti iye anachimwa ndipo ankafunika kukhululukidwa ndi Mulungu. Mosachedwa, iye anakhulupirira kuti Khristu anamufera. (<b>Machitidwe 8:32-35</b>)</li><li>• Filipino anamubatiza chomwe ndi chizindikiro chakuti ndi wotsatira Yesu (<i>Fotokozani za ubatizo</i>). (<i>Fotokozani za kusinthika kwake ndi chimwemwe chimene anali nacho tsopano m'moyo mwake.</i>)</li><li>• Mzimu Woyera anatenga Filipino ndi kupita naye kuti akawuzenso ena za Yesu. (<b>Machitidwe 8:36-40</b>)</li><li>• <i>Mulungu akufuna kuti munthu aliyense adziwe kuti Yesu anafa pa mtanda chifukwa cha machimo athu. Yankhulani za anthu amene amatithandiza kuti timvetse zomwe zili m'Baibulo. Ife tikuyenera kuyamika chifukwa tinamva nkhanu yabwino ya Yesu.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Filipino afalitsa uthenga wabwino.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Machitidwe 8:35</b> .
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi mngelo anawuzira Filipino kuti apite kuti?</li><li>• Kodi munthuyo anali wochokera m'dziko liti?</li><li>• N'chifukwa chiyani Filipino anapita kumene kunali munthuyo?</li><li>• Kodi iye ankawerenga nkhanu ya ndani?</li><li>• Kodi munthuyo anachita chiyani Filipino atamufotokozerira za Yesu?</li><li>• Kodi anabatizidwa kuti?</li><li>• Kodi iye anamva bwanji mu mtima mwake pamene ankapita kwawo?</li><li>• Kodi machimo athu angakhulukidwe motani?</li></ul>

## A10 Nkhani Yachitatu

**Saulo ndi kuwala kwakukulu - Iyi ndi nkhani ya mphamvu ya Mulungu yosintha miyoyo.**

<b>MAWU OYAMBA</b>	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"> <li>• Yesu amakonda munthu aliyense ndipo anafera aliyense, ngakhale anthu amene amadana naye.</li> <li>• Ndi Yesu yekha amene ali ndi mphamvu zosintha miyoyo yathu.</li> </ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 9:1-9</i>  <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>2 Akorinto 5:17</i></p>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"> <li>• Saulo anali Myuda amene ankadana ndi Yesu. Iye ankadana ndi otsatira a Yesu ndipo ankafuna kuti onse aphedwe. Fotokozani kumene anali nthawi imene Stefano ankaphedwa ndi miyala. (Nkhani Yoyamba)</li> <li>• Funsani ana ngati akanakonda kuti Saulo akhale mnzawo? Chifukwa chiyani? Ngati si choncho, ndi chifukwa chiyani?</li> </ul> <ul style="list-style-type: none"> <li>• Tsiku lina Saulo ananyamuka ulendo wopita ku mzinda wa Damasiko kukamanga ndi kuyika m'ndende Akhristu. (<b>Machitidwe 9:1-2</b>) <i>Kambiranani zomwe Saulo ankamva mu mtima mwake ndi maganizo ake pamene ankayenda.</i></li> <li>• Ali pafupi kufika ku Damasiko, mwadzidzidzi kuwala kwakukulu kunamuzungulira ndipo anagwa pansu. <i>Gwiritsani ntchito mawu amene Saulo anamva ndi yankho lake. Fotokozani zomwe Saulo ankamva mu mtima mwake nthawi imeneyi. (Machitidwe 9:3-4)</i></li> <li>• Mawu anayankha kuti anali Yesu. <i>Fotokozani zomwe Saulo anazindikira tsopano – Yesu ndi Mwana wa Mulungu, ndipo Iye ali moyo. Zomwe ankaganiza za Yesu zinali zolakwika! Yesu anawuza Saulo kuti alowe mu mzinda wa Damasiko kumene adzauzidwa zoti achite. Anthu amene anali ndi Saulo anadabwa pamene ankamva mawu koma wosamuona amene akuyankhula. (Machitidwe 9:5-7)</i></li> <li>• Pamene Saulo anayimirira anali wakhungu ndipo anamugwira dzanja ndi kulowa naye mu mzinda. Iye anakhala wosaona kwa masiku atatu ndipo sanadye kapena kumwa kanthu. (<b>Machitidwe 9:8-9</b>) <i>Kodi mukuganiza kuti anamva motani mu mtima mwake pozindikira kuti sakuonanso?</i></li> <li>• <i>Kambiranani chifukwa chomwe Ambuye Yesu anakumana ndi Saulo pa njira. Kumbutsani ana kuti Saulo ankadana ndi Yesu pamodzi ndi omutsatira ake. Iye ankafuna kuti onse aphedwe koma Yesu anamukonda ndipo anafuna kuti iye akhale womutsatira wake ngakhale sanali munthu woyenera. Ambuye Yesu anafuna kusintha moyo wake kwathunthu.</i></li> <li>• <i>Ife tikufunika Ambuye Yesu kuti achotse machimo athu ndi kutipatsa mphamvu yokhala moyo watsopano.</i></li> </ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Saulo ndi kuwala kwakukulu/Saulo aona kuwala kwakukulu.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>2 Akorinto 5:17.</b></p> <p>Fananizani moyo wakale wa Saulo ndi moyo umene anali nawo “mwa Khristu” chifukwa miyoyo yathu imasinthika ndi kukhala yatsopano.</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"> <li>• Kodi Saulo ankapita kuti?</li> <li>• N'chifukwa chiyani anali pa ulendo umenewu?</li> <li>• Kodi iye anaona ndani?</li> <li>• Kodi iye anamva chiyani?</li> <li>• Kodi mawuwo ankati chiyani?</li> <li>• Kodi Saulo anazindikira chiyani atadziwa kuti anali Yesu amene ankayankhula kwa iye?</li> <li>• Kodi ndi chiyani chomwe Saulo sanachite kwa masiku atatu?</li> <li>• Kodi ndi ndani yekha amene angatipatsa mphamvu zokhala moyo watsopano?</li> </ul>

## A10 Nkhani Yachinayi

### Kusinthika kwa Saulo - Iyi ndi nkhani ya momwe Mulungu anasinthira Saulo.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Mulungu akufuna kuti atithandize ndi kutumiza anthu kwa ife pamene tikuwafuna.</li><li>• Monga Saulo, Mulungu amasintha miyoyo ya anthu lero ndipo amawathandiza kuti akhale ofunikira kwa Iye.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 9:10-23</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 9:20</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Bwerezani kuona gawo loyamba la nkhani ya Saulo – kodi mukukumbukira chomwe Saulo “wakale” anali? Kodi otsatira a Yesu amene anali mu Damasiko ankamva bwanji m’mitima mwa za Saulo “wakale”? (Ankachita mantha...)</li><li>• Mulungu ankayenera kukwakonzekeretsa kuti athe kumvomereza Saulo kukhala mmodzi wa iwo m’banja lake. Tiyeni tione zomwe zinachitika...</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Mulungu anayankhula ndi Ananiya ku maloto ndipo anamuwuzwa kuti apite kumene kunali Saulo. (<i>Machitidwe 9:10-12</i>) Kodi mukuganiza kuti Ananiya ankafuna kupita? Ngati si choncho ndi chifukwa chiyani?</li><li>• Ananiya anakachita mantha kuti mwina Saulo akamugwira kapena kumupha. Mulungu anamuwuzwa kuti asadandaule chifukwa Iye wasankha Saulo kuti agwire ntchito yake - kuti akawuze anthu za Mulungu kwa amene sanamvepo za Mulunguyo. (<i>Machitidwe 9:13-16</i>)</li><li>• Ananiya anamvera ndipo anapita kwa Saulo. Iye anamutcha m’bale (<i>fotokozani chifukwa chomwe analili abale</i>) ndipo anamuwuzwa kuti anatumidwa ndi Ambuye Yesu. Iye anakhudza maso a Saulo kuti iye aonenso. Saulo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Iye anabatizidwa ndipo anadya chakudya. (<i>Machitidwe 9:17-19a</i>) Kodi anamva bwanji mu mtima mwake Ananiya atabwera kumene anali?</li><li>• Pasanapite nthawi Saulo anakumana ndi ena mwa otsatira Yesu mu Damasiko. Nthawi yomweyo anayamba kulalikira za Ambuye Yesu. <i>Fotokozani zomwe anakachita anthu amene anakumana ndi Saulo mu Damasiko. Iwo sanayembekezere kuti Saulo angakhale munthu wotere!</i></li><li>• Ayuda amene anamva za kusinthika kwa Saulo sanakondwere ndi uthenga umene ankalalikira ndipo anakonza chiwembu choti amuphe. Saulo anathawa mu Damasiko potsitsidwa pa khoma ali m’dengu nthawi ya usiku. (<i>Machitidwe 9:19-25</i>) <i>Fotokozani za kusinthika kwa moyo wa Saulo ndi zomwe zinachitika kuti atakhala wokhulupirira Yesu.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Kusinthika kwa Saulo/Kusandulika mtima kwa Saulo.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <i>Machitidwe 9:20</i> .
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi Mulungu anayankhula Ananiya m’njira yanji?</li><li>• N’chifukwa chiyani Ananiya anakachita mantha ndi Saulo?</li><li>• Kodi ntchito yatsopano ya Saulo inali yotani?</li><li>• Kodi chinachitika ndi chiyani m’maso mwa Saulo pamene Ananiya anamukhudza?</li><li>• Kodi Saulo analandira mphatso ina iti pamene Ananiya anabwera kwa iye?</li><li>• Kodi nthawi yomweyo Saulo anayamba kuchita chiyani?</li><li>• N’chifukwa chiyani Saulo anathawa ali m’dengu?</li><li>• Kodi miyoyo yathu ingasinthike motani ngati unachitira moyo wa Saulo?</li></ul>

## A11 Nkhani Yoyamba

Paulo (Saulo) ku Antiokeya - Iyi ndi nkhani ya kuthandiza pa ntchito ya Mulungu.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Anthu amene amakhulupirira Yesu amatchedwa “Akhristu.”</li><li>• Mulungu ali ndi chikonzero chapadera pa ife pamene tamukhulupirira Iye - Iye amafuna kuti tikhale omuthandiza.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 11:19-30</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 11:26</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Funsani ana momwe angathandizire pa zochitika zosiyanasiyana – Kodi mungathandize motani aphunzitsi anu? Kodi mungathandize motani ku nyumba kwanu pamene mayi anu akudwala?</li><li>• Fotokozani kuti nkhani ya lero ndi ya anthu awiri amene akuthandiza pa ntchito ya Mulungu.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Uthenga wabwino wa Yesu unafalitsidwa ndipo mpingo wa Mulungu unakula. Okhulupirira ena anapita kukhala mu mzinda wa Antiokeya. Kumeneko, iwo anatha kufotokozera anthu amene sanamvepo Uthenga Wabwino ndipo anthu ambiri anakhulupirira Ambuye Yesu. <b>(Machitidwe 11:19-21)</b></li><li>• Mosachedwa mpingo wa ku Yerusalemu unamva za zinthu zazikulu zomwe zinkachitika ku Antiokeya. <i>Kodi okhulupirira anamva bwanji m’mitima mwawo? (Anasangalala.)</i> Iwo anagwirizana zotumiza Barnaba kuti akamve zambiri. Iye anapita ku Antiokeya ndipo anali wosangalala kupeza kuti kunali okhulupirira atsopano ambiri. Barnaba anayesa kuwaphunzitsa okhulupirira atsopanowa ndi kuwalimbikitsa kuti azikonda Ambuye Yesu. <b>(Machitidwe 11:22-24)</b> <i>Kodi Barnaba anali munthu wa mtima wotani?</i></li><li>• Barnaba anali wotanganidwa kwambiri ku Antiokeya ndipo ankafuna wina woti azimuthandiza. Mulungu anamukumbutsa za Saulo, amene anali atakumana naye kale. Saulo atakumana ndi Ambuye Yesu, iye anabwerera ku Tarisi, ku mzinda umene anabadwira. Barnaba anapita ku Tarisi ndipo anakamutenga Saulo ndi kubwera naye ku Antiokeya kuti adzathandizane ntchito. <b>(Machitidwe 11:25-26)</b></li><li>• <i>Fotokozani kuti Antiokeya anali malo ofunika kwambiri kwa Saulo/Paulo chifukwa ndi kumene anayambira utumiki wake. Uwu unali utumiki wapadera umene Mulungu anamukonzera.</i> Saulo ndi Barnaba anakhala chaka chonse ku Antiokeya, kuphunzitsa okhulupirira kumeneko. Pa nthawi imeneyi, okhulupirira Yesu Khristu anayamba kutchedwa “Akhristu.” <b>(Machitidwe 11:26)</b></li><li>• <i>Pamene ife takhulupirira Yesu timayamba kutchedwa “Akhristu.” Timapatsidwa dzina lake! Mulungu ali ndi cholinga chapadera ndi Akhristu onse, monga mmene zinalili ndi Paulo. Iye akufuna Akhristu akhale omuthandiza ake.</i></li><li>• <i>Onetsani kuti ana akumvetsa tanthauzo lokhala Mkhristu.</i></li><li>• <i>Kambiranani momwe Mulungu angatigwiritsire ntchito Akhristu monga omuthandiza ake.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Paulo (Saulo) ku Antiokeya.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Machitidwe 11:26.</b>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi ndi mzinda uti kumene mpingo unakula?</li><li>• Kodi anthu a ku Yerusalemu anatumiza ndani ku Antiokeya?</li><li>• Kodi Barnaba anachita chiyani ku Antiokeya?</li><li>• Kodi Barnaba ankafuna chiyani msangamsanga kumeneko?</li><li>• Kodi Barnaba anapita kukafunafuna ndani?</li><li>• Kodi Saulo ndi Barnaba anakhala nthawi yayitali yotani ku Antiokeya?</li><li>• Kodi anthu amene anakhulupirira Yesu anawapatsa dzina lanji?</li><li>• Kodi Saulo ankagwira ntchito ya ndani?</li></ul>

## A11 Nkhani Yachiwiri

### Paulo (Saulo) ku Kupro - Iyi ndi nkhani ya kuwuzana ena za Yesu.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Ife tikuyenera kuchita chisankho choyenera chokhulupirira Yesu.</li><li>• Ife tikuyenera kuwuzana anthu ena za Yesu.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 13:1-12</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Mateyu 28:19</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Thandizani kuti ana awiriawiri agwire ntchito yoganiza zinthu zambiri za Yesu.</li><li>• Fotokozerani ana kuti nkhani ya lero ndi ya Paulo (fotokozani za kusintha kwa dzina), Barnaba ndi Yohane Marko, akuwuzana anthu za Yesu. Mutha kulemba mainawo pa bodi kapena pa chipepala. Lembani mwachidule zonse zimene apeza ndipo fotokozani kuti ndi zofunika kuti aliyense adziwe za Yesu ndi zomwe anachita.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Tsiku lina Akhristu a ku Antiokeya anasonkhana pamodzi. Paulo ndi Barnaba anali nawo. Mzimu Woyera anafotokozana momveka bwino kwa atsogoleri enawo kuti Barnaba ndi Paulo ankayenera kupita kukagwira ntchito ya Mulungu ya padera. Iwo atapemphera pa nkhani imeneyi, Barnaba, Saulo ndi Yohane Marko, amene anali mphwake wa Barnaba, anayamuka pa bwato ulendo wopita ku chilumba cha Kupro. (<b>Machitidwe 13:1-4</b>)</li><li>• Pamene anafika kumeneko, iwo anayendayenda kumalalikira nkhani yabwino ya Yesu. Pa malo ena wotchedwa Pafo anakumana ndi munthu wamatsenga amene anali wotumikira bwanamkubwa wa ku Kupro. Bwanamkubwa anamva za Barnaba ndi Saulo ndipo anafuna kukumana nawo. Iye anamva Mawu a Mulungu koma Elimasi, wamatsengayo, anayesetsa kumuletsa kuti asakhulupirire. (<b>Machitidwe 13:5-8</b>)</li><li>• Saulo anazindikira kuti wamatsengayo ankachita zinthu zoyipa. Saulo anali wodzazidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera. Iye anayang'anitsitsa wamatsengayo ndi kumuwuzana kuti ankachita zinthu zoyipa ndipo Ambuye achititsa kuti akhale wosaona. Paulo atangoyankhula mawu amenewa, Elimasi sanathenso kuona ndipo ankayenda osona kumene akupita ndipo anapeza wina womuthandiza kupita kumene akufuna. (<b>Machitidwe 13:9-11</b>) <i>Fotokozani kuti ndi zolakwika kutsutsana ndi Ambuye Yesu.</i></li><li>• Bwanamkubwa anaona ukulu wamphamvu ya Mulungu ndipo iye anakhulupirira Yesu. (<b>Machitidwe 13:12</b>)</li><li>• <i>Paulo, Barnaba, Yohane Marko ndi bwanamkubwa anachita chisankho cholondola pokhulupirira Yesu. Elimasi anachita chisankho cholakwika. Yesu akufuna kuti ifenso timukhulupirire.</i></li><li>• <i>Kodi mukudziwa wina amene amawuzana anthu za Yesu ku dera lina?</i></li><li>• <i>Kodi inu mungawuze bwanji anthu ena za Yesu?</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Paulo (Saulo) ku Kupro.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Mateyu 28:19</b>.</p> <p>Fotokozani kuti awa ndi mawu a Yesu asanabwerere Kumwamba. Chinali cholinga chake kuti anthu kulikonse (mayiko onse) amve Uthenga Wabwino ndi kukhulupirira Iye.</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi ndi ndani amene anatuma Paulo ndi Barnaba kuti akagwire ntchito ya padera?</li><li>• Kodi ndi ndani anapita nawo?</li><li>• Kodi iwo anayenda motani?</li><li>• Kodi dzina la chilumba chimene anapitako linali chiyani?</li><li>• Kodi ku Pafo anakumana ndi ndani?</li><li>• Kodi ndi ndani amene anakhulupirira Yesu ku Pafo?</li><li>• Kodi chinachitika ndi chiyani kwa munthu wamatsenga uja?</li><li>• Kodi ndi ndani amene anayankhula mawu amene ali pa Vesi Yoloweza?</li></ul>



## A11 Nkhani Yachitatu

Paulo akumana ndi Lidiya - Iyi ndi nkhani ya mayi amene anakhulupirira Yesu.

	<p><b>Ife tikuphonzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Paulo ndi anzake anatsogozedwa ndi Mzimu Woyera kuti awuze anthu za Yesu.</li><li>• Munthu aliyense atha kumva uthenga wa Yesu ndi kukhulupirira.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 16:6-15</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 2:21</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Funsani kuti akuwuzeni nthawi imene anayenda ulendo wautali kupita ku malo ena. Kodi anapita kuti? Kodi anayenda kwa nthawi yayitali bwanji? Kodi kumeneko anakaona ndani?</li><li>• Fotokozani kwa ana kuti nkhani ya lero ndi ya Paulo ndi anzake ali pa ulendo.</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Paulo ndi anzake awiri Sila ndi Timoteyo anayenda mtunda wautali kwambiri, kuchoka dziko lina kupita ku dziko lina. Mzimu Woyera anawaonetsa malo enieni amene Mulungu ankafuna kuti apite. Kulikonse kumene iwo ankapita kunali anthu ambiri amene ankayenera kuti amve za Ambuye Yesu. (<b>Machitidwe 16:6-8</b>)</li><li>• Kenaka anafika m'tauni ya m'mbali mwa nyanja. Usiku umenewo Paulo anali ndi maloto apadera kwambiri pamene anaona munthu wa ku Makedoniya akumudandaulira kuti apite kwa anthu kumeneko. Paulo anazindikira kuti Mulungu akumonetsa momveka bwino kumene akuyenera kupita tsopano. (<b>Machitidwe 16:9-10</b>) <i>Fotokozani kuti Mulungu ankafuna kuti anthu akumeneko akamve za Yesu motero Iye anatuma Paulo ndi anzakewo. Mulungu saona za dera limene ife timakhala. Iye amafuna kuti munthu aliyense amve za Iye.</i></li><li>• Mofulumira anapeza bwato limene linkapita kumeneko. Mosachedwa anafika mu mzinda waukulu wotchedwa Filipi. Pa tsiku la Sabata, Paulo ndi anzake anapita kunjira kwa mzindawo m'mbali mwa mtsinje. Kumeneko iwo anapeza amayi amene anabwera kudzapemphera. (<b>Machitidwe 16: 11-13</b>) <i>Amayi amenewa ku mtsinjeko ankapemphera kwa Mulungu. Kodi Mulungu tingamayankhule naye kuti? (Fotokozani kwa ana kuti titha kuyankhula ndi Mulungu malo ena aliwonse.)</i></li><li>• Mmodzi mwa amayi amenewa anali Lidiya. Iye ankagulitsa nsalu za purple. Iye anali atakhulupirira Mulungu kwa nthawi yayitali koma anali asanamve za Mwana wa Mulungu, Ambuye Yesu. Lidiya anamvetsera mwachidwi zonse zimene Paulo anayankhula. Iye anadziwa mu mtima mwake kuti zimene ankamva zinali zoona ndipo anakhulupirira Ambuye Yesu. Iye anali wokondwa kwambiri kuti Paulo anabwera mu mzindamo. (<b>Machitidwe 16:14-15</b>) <i>Banja la Lidiya linakhala Akhristu. Onse anabatizidwa ndipo Lidiya anayitana Paulo ndi anzake kuti akakhale m'nyumba mwake.</i></li><li>• <i>Yankhulani za kusintha kumene kunabwera pamene Lidiya ndi banja lake anakhulupirira Yesu. Fotokozani kuti munthu akakhala wokhulupirira mwa Yesu, munthuyo amasinthika.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Paulo akumana ndi Lidiya.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Machitidwe 2:21</b>.</p> <p>Fotokozani kuti kuyitana pa dzina la Yesu zimatanthauza kumupempha kuti atipulumutse ku machimo athu. Izi ndi zimene anachita Lidiya mu nkhani yathu.</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Tchulani mayina a anzake a Paulo.</li><li>• Kodi ndi ndani amene anawaonetsa komwe Mulungu ankafuna kuti apite?</li><li>• Kodi chinachitika ndi chiyani m'maloto a Paulo?</li><li>• Kodi Paulo ndi anzake anayenda motani ulendo wopita ku Makedoniya?</li><li>• Kodi Paulo ndi anzake anakumana ndi amayi aja kuti?</li><li>• Kodi iwo ankachita chiyani?</li><li>• Kodi Lidiya ankagwira ntchito yanji?</li><li>• Kodi Lidiya anachita chiyani atamva za Yesu?</li></ul>

## A11 Nkhani Yachinayi

Paulo ndi Sila m'ndende - Iyi ndi nkhani ya anthu ambiri kukhulupirira Yesu.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Tikuyenera kukhulupirira Ambuye Yesu kuti tipulumutsidwe.</li><li>• Kukhala Mkhristu kumasintho moyo wa munthu.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Machitidwe 16:16-34</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Machitidwe 16:31</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Funsani ana kuti akufotokozereni chomwe chimawasangalatsa.</li><li>• Fotokozerani ana kuti mu nkhani ya lero muli anthu osangalala. Awuzeni kuti amvetsere mwachidwi kuti apeze amene akusangalala...</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Tsiku lina, pamene Paulo ndi Sila anali ku Filipi, anathandiza mtsikana amene anali kapolo. Izi zinakwiyitsa kwambiri mabwana ake ndipo anakokera Paulo ndi Sila ku bwalo la msika ndipo anawanenera mabodza. (<i>Machitidwe 16:16-21</i>) <i>Kambiranani momwe Paulo ndi Sila ankamvera m'mitima mwawo.</i></li><li>• Paulo ndi Sila anamenyedwa ndipo kenaka anaponyedwa m'ndende. Woyang'anira ndende anamanga manja awo ndi maunyolo ndipo miyendo yawo analowetsa mu zibowo za m'matabwa. (<i>Machitidwe 16:22-24</i>) <i>Kambiranani inso momwe ankamvera Paulo ndi Sila m'mitima mwawo.</i></li><li>• Pakati pa usiku, a m'ndende anzawo anamva Paulo ndi Sila akupemphera ndi kuyimba nyimbo kwa Mulungu! Ngakhale misana yawo inali ndi mabala chifukwa cha kukwapulidwa, iwo anatamandabe Mulungu. (<i>Machitidwe 16:25</i>) <i>Kodi a m'ndende anzawo anaganiza chiyani?</i></li><li>• Mwadzidzidzi kunamveka phokoso. Chilichonse chinanjenjemera ndi kugwedera. Zitseko zinatsekuka ndipo maunyolo anaduka. Ichi chinali chivomerezi. (<i>Machitidwe 16:26</i>)</li><li>• Woyang'anira ndende atadzuka anaona kuti zitseko zonse za ndende zinali zotsekuka. <i>Kodi chimene iye anayamba kuganiza chinali chiyani? Iye anaganiza kuti adzaphedwa ngati a m'ndende onse athawa. Paulo anamuwuzwa kuti asadandaule chifukwa a m'ndende onse analipo. (Machitidwe 16:27-28)</i></li><li>• Woyang'anira ndende anzindikira kuti anali wochimwa. Iye anafunsa Paulo chomwe ankayenera kuchita kuti apulumuke. Paulo anayankha kuti "Khulupirira Ambuye Yesu ndipo udzapulumuka." Paulo ndi Sila anafotokozerwa woyang'anira ndendeyo ndi banja lake kuti Yesu anafa pa mtanda chifukwa cha machimo awo. Woyang'anira ndende anatenga Paulo ndi Sila ndi kupita nawo ku nyumba yake, iye anatsuka mabala awo ndi kuwapatsa chakudya. Iyi inali nthawi ya chisangalalo kwa woyang'anira ndende ndi banja lake chifukwa anakhulupirira Yesu. (<i>Machitidwe 16:29-34</i>)</li><li>• <i>Kodi anali wosangalala m'nkhani imeneyi ndi ndani? N'chifukwa chiyani anali osangalala? (Limbikitsani ana kuti afotokoze za Paulo ndi Sila, komanso za woyang'anira ndende ndi banja lake. Afotokozereni kuti anthu amenewa anali wosangalala chifukwa Ambuye Yesu anawapulumutsa.)</i></li><li>• <i>Fotokozerani ana kuti tikuyenera kupulumutsidwa ku machimo athu. Ife tikhulupirire Yesu chifukwa ndi Mwana wa Mulungu amene anatifera.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Paulo ndi Sila m'ndende.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <i>Machitidwe 16:31.</i>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi Paulo ndi Sila anathandiza ndani?</li><li>• Kodi chinachitika ndi chiyani kwa Paulo ndi Sila?</li><li>• Kodi Paulo ndi Sila ankachita chiyani pakati pa usiku?</li><li>• Kodi chinachitika ndi chiyani pamene iwo ankayimba?</li><li>• N'chifukwa chiyani woyang'anira ndende anali ndi mantha kutachitika chivomerezi?</li><li>• Kodi woyang'anira ndende anafunsa Paulo ndi Sila chiyani?</li><li>• Kodi Paulo ndi Sila anamuwuzwa chiyani?</li><li>• Kodi woyang'anira ndendeyo anachita chiyani usiku umenewu?</li><li>• Kodi iye anaonetsa motani kuti moyo wake wasintho?</li></ul>

## A12 Nkhani Yoyamba

### Zakariya ndi Elizabeti - Iyi ndi nkhani ya Mulungu kuyankha pemphero.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Mulungu amayankha pemphero.</li><li>• Mapemphero amayankhidwa pa nthawi ya Mulungu, osati yathu.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Luka 1:5-25</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Luka 1:13</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Funsani ana kuti afotokoze za mabanja awo. Kambiranani nawo za ana aang'ono amene ali m'banja mwawo kapena pakati pa abale awo. Mwana wakhanda amabweretsa chimwemwe m'banja.</li><li>• Funsani ana kuti aganizire za chinthu chimene amachikonda. Kodi iwo angafotokoze chifukwa chomwe amachikondera? Banja limene lili m'nkhani yathu ya lero nalonso linkamva zimenezi mu mtima mwawo; iwo ankafuna mwana!</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Zakariya ndi Elizabeti akanakonda akanakhala ndi mwana. Pamene anakula, anzawo ambiri anayamba kubereka ana koma iwo analipo awiri okha basi. <i>Kodi inu mukuganiza kuti ankamva bwanji mu mtima mwawo? Kodi ndi chiyani chomwe chinkasowa pakati pa Zakariya ndi Elizabeti chifukwa chopanda ana? (Lolani ana kuti afotokoze zimenezi molinga ndi zomwe zimachitika pakati pawo ndi pa chikhalidwe chawo.) (Luka 1:5-7)</i></li><li>• Iwo anaganiza zopemphera kwa Mulungu. Iwo ankadziwa kuti Mulungu amayankha pemphero! <b>(Luka 1:13)</b> <i>Fotokozani kuti tingathe kupempherera vuto lina lililonse limene tingakhale nalo.</i></li><li>• Mulungu anamva pemphero lawo ndipo anatuma mngelo kuti adzakumane ndi Zakariya pamene ankagwira ntchito m'Nyumba ya Mulungu. <i>Kodi mukuganiza kuti Zakariya anamva bwanji mu mtima mwake pamene anaona mngeloyo? Mngelo anamuwuzwa kuti asachite mantha, kenaka anamuwuzanso nkhani yabwino yoti Elizabeti anadzabereka mwana wamwamuna ndipo adzamutcha Yohane. (Luka 1:8-11)</i></li><li>• Zakariya sanakhulupirire nkhani imene anawuzidwa. Iye anaganiza kuti popeza iye ndi Elizabeti anali okalamba, sizikanatheka kubereka mwana. Mngelo anamuwuzwa kuti popeza sanakhulupirire uthenga wochokera kwa Mulungu, sadzatha kuyankhula mpaka mwanayo atabadwa. <b>(Luka 1:18-20)</b></li><li>• <i>Titha kuphunzira phunziro lofunika kwambiri kuchokera kwa Zakariya... Pamene tapemphera tikuyenera kukhulupirira kuti Mulungu adzayankha mapemphero athu.</i></li><li>• <i>Ganizira zinthu zina zomwe mungapempherere lero!</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Zakariya ndi Elizabeti.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Luka 1:13.</b>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi mkazi wa Zakariya anali ndani?</li><li>• Kodi banja limeneli linkafuna chiyani?</li><li>• Kodi Zakariya ndi Elizabeti anapemphera kwa ndani?</li><li>• Kodi ndi ndani amene anabwera kudzakumana ndi Zakariya m'Nyumba ya Mulungu?</li><li>• Kodi Zakariya anamva bwanji mu mtima mwake pamene anaona mngelo?</li><li>• Kodi uthenga wochokera kwa mngelo unali wotani?</li><li>• Kodi chinachitika ndi chiyani kwa Zakariya chifukwa chosakhulupirira uthengawo?</li><li>• Pamene tapemphera, kodi chinthu chofunika chomwe tikuyenera kuchita ndi chiyani?</li></ul>

## A12 Nkhani Yachiwiri

Mariya ndi Gabrieli - Iyi ndi nkhani ya Mariya kukhulupirira zimene Mulungu wanena.

	<p><b>Ife tikuphonzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Mariya anakhulupirira uthenga wa mngelo ngakhale zinkaoneka ngati zosatheka.</li><li>• Mulungu atha kuchita zinthu zomwe zikuoneka ngati zosatheka.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Luka 1:26-38</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Luka 1:37</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<p>Bwerezani kuona nkhani ya sabata latha ya uthenga wa mngelo kwa Zakariya ndi Elizabeti wakuti adzakhala ndi mwana. izi zitangochitika, Mulungu anatumanso mngelo ndi uthenga wapadera kwa munthu wina.</p>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• <i>Siyantsani pakati pa Mariya ndi Elizabeti.</i> Mariya anali mtsikana wamng'ono, amene anali pa ubwenzi ndi Yosefe ndipo ankakhala ku Nazareti. Tsiku lina kunabwera mngelo dzina lake Gabrieli. <b>(Luka 1:26-27)</b> Thandizani ana kuti amvetse kuti izi sizinkachitika nthawi zonse ndiponso kuti Mariya anali ndi mantha.</li><li>• Mngelo anamuwuzwa kuti asachite mantha. Iye anamvetsera mwachidwi zomwe mngelo Gabrieli ankamuwuzwa kuti adzakhala ndi mwana wamwamuna. Mariya anadabwa pang'ono; iye analibe mwamuna nthawi imeneyi. Mngelo anamuwuzwa kuti Mulungu Mzimu Woyera ndiye amene adzakupatse mwana wapadera ameneyu. Iye adzakupatse dzina lakuti Yesu. <b>(Luka 1:29-34)</b></li><li>• Yesu adzakhala wamkulu kuposa mwana wina aliyense amene anabadwapo. Iye adzatchedwa Mwana wa Mulungu. Izi mwina zinali zovuta kuzimvetsa koma mngelo anawuzwa Mariya kuti palibe chinthu chosatheka ndi Mulungu. <b>(Luka 1:35-37)</b></li><li>• Mariya anakhulupirira uthenga umene anawuzidwa. Mariya anali wokonzeka kukwaniritsa chikonzero chachikulu cha Mulungu chotumiza Mwana wake pa dziko lapansi. Kubadwa kwa Yesu kudzakhala chodabwitsa chachikulu. <b>(Luka 1:38)</b></li><li>• <i>Kodi wina anakulonjezanipo kanthu zomwe zinali zovuta kwa inu kukhulupirira?</i></li><li>• <i>Kodi n'chifukwa chiyani mukuganiza kuti anakhulupirira? Mulungu amafuna aliyense wa ife kuti tizimukhulupirira monga anachitira Mariya.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Mariya ndi Gabrieli/Mariya ndi Mngelo Gabrieli.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Luka 1:37.</b></p> <p>Kodi ana angatchulepo zinthu zina “zosatheka” zomwe Mulungu anachita m'Baibulo? Mutamandeni pakuti Iye ndi Mulungu wamphamvu!</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi Mariya ankakhala kuti?</li><li>• Kodi Mariya anali pa ubwenzi ndi yani?</li><li>• Kodi mngelo amene anabwera kwa Mariya dzina lake anali ndani?</li><li>• N'chifukwa chiyani Mariya anadabwa pang'ono ndi uthenga wochokera kwa mngelo?</li><li>• Kodi mwana ameneyu adzakhala wapadera motani?</li><li>• Kodi Mariya anachita chiyani ndi uthengawu?</li><li>• Kodi Mariya ndi chitsanzo chabwino motani choti titsatire?</li><li>• Kodi ndi zinthu ziti zosatheka ndi Mulungu?</li></ul>

## A12 Nkhani Yachitatu

Kubadwa kwa Yohane - Iyi ndi nkhani ya Mulungu kusunga malonjezo ake.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Mulungu anasunga lonjezo lake kwa Zakariya ndi Elizabeti.</li><li>• Mulungu amasunga malonjezo ake kwa ifenso.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Luka 1:57-80</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Luka 1:76</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kambiranani momwe mungamvere mu mtima mwanu ngati mutakhala miyezi yambiri wosayankhula. Kodi inu mungamayankhulane ndi anthu motani? Ana akhale awiriawiri ndipo ayese kumayankhulana pogwiritsa ntchito zizindikiro. Mwana woyamba apatsidwe malangizo osavuta/nkhani yoti awuze mwana wachiwiri. (Chitsanzo: Kunja kukugwa mvula.) Bwerezani koma asinthe zochita. Kumbutsani ana kuti izi ndi zimene zinachitika kwa Zakariya pamene sanakhulupirire uthenga wa mngelo uja.</li><li>• Kodi mmawa wa tsiku la Khristmasi kapena tsiku lanu lobadwa mumamva bwanji mu mtima mwanu mukamalandira mphatso zimene mwakhala mukuziyembekezera? Umu ndi mmene Zakariya ndi Elizabeti anamvera mu mtima mwawo pamene mwana wawo anabadwa monga momwe mngelo analonjezera. Inali nthawi yopambana kwambiri!</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Pamene mwana anabadwa abale ndi anansi awo ankafuna kuti amupatse dzina la abambo ake Zakariya. Elizabeti anawawuza kuti dzina lake ndi Yohane. <b>(Luka 1:57-60)</b> <i>N'chifukwa chiyani Elizabeti ananena kuti adzatchedwa Yohane?</i></li><li>• Pamene anafunsa Zakariya za dzina la mwanayo, iye analemba kuti "Dzina lake ndi Yohane." <b>(Luka 1:62-63)</b></li><li>• Nthawi yomweyo iye anayambanso kuyankhula. Zakariya anayamika ndi kutamanda Mulungu. <i>N'chifukwa chiyani Zakariya anachita zimenezi? Mulungu anakwaniritsa lonjezo lake: iye anali wodzaza ndi chimwemwe mwana wake atabadwa ndipo anazindikira kuti Mulungu adzachita zinthu zazikulu kwambiri!</i> Munthu aliyense anadabwa chifukwa cha zimene anazionazo. <b>(Luka 1:64-66)</b></li><li>• Yohane anali mwana wosiyana ndi ena. Chifukwa chiyani? <i>Kumbutsani ana kuti makolo ake anadikira zaka zambiri kuti abadwe koma chofunikanso kwambiri iye adzakhala munthu amene adzakonza njira pa kubwera kwa Ambuye Yesu.</i></li><li>• <i>Mulungu adzasunganso malonjezo ake kwa ifenso. Tchulani malonjezo angapo amene iye akulonjeza m'Baibulo.</i></li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Kubadwa kwa Yohane.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Luka 1:76.</b></p> <p>Fotokozani kuti vesi iyi ndi gawo limodzi la nyimbo yomwe Zakariya anayimba kutamanda Mulungu.</p>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi mwamuna wa Elizabeti anali ndani?</li><li>• N'chifukwa chiyani sankatha kuyankhula?</li><li>• Kodi anansi ankafuna kuti mwanayo dzina lake likhale ndani?</li><li>• N'chifukwa chiyani Zakariya ndi Elizabeti anamupatsa dzina loti Yohane?</li><li>• Kodi Zakariya anayamba kuyankhulanso liti?</li><li>• Kodi Yohane ankayenera kugwira ntchito yapadera iti?</li></ul> <p><b>Pangani:</b> Ana apange kadi ya tsiku lobadwa Yohane.</p>

## A12 Nkhani Yachinayi

Kubadwa kwa Yesu - Iyi ndi nkhani ya Mulungu kupereka Mwana wake kukhala Mpulumutsi wathu.

	<p><b>Ife tikuphunzira kuti:</b></p> <ul style="list-style-type: none"><li>• Yesu ndi Mwana wa Mulungu amene anabwera kudzakhala Mpulumutsi wathu.</li><li>• Ife tikuyenera kuyamika Mulungu chifukwa cha chikondi chake chachikulu potumiza Ambuye Yesu.</li></ul> <p><b>Ndime Yowerenga:</b> <i>Luka 2:1-7</i> <b>Vesi Yoloweza:</b> <i>Luka 2:7</i></p>
<b>MAWU OYAMBA</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Fotokozani kuti zinthu zimatha kusintha nthawi yothayitha. Perekani chitsanzo chogwirizana ndi zomwe zikuchitika, zomwe zikuchitikira ana kapena inuyo.</li><li>• Fotokozani kuti nthawi iyi mwana wa Mariya anali pafupi kubadwa. Zikanakhala zosavuta ngati mwanayo akanabadwira ku Nazareti kumene Yosefe ndi Mariya ankakhala, koma...</li></ul>
<b>PHUNZITSANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kaisara wa Chiroma analamula kuti anthu onse apite ku madera amene anabadwira kuti akalembetse mayina awo. Yosefe ndi Mariya anapita ku Betelehemu. <b>(Luka 2:1-5)</b> Fotokozani kutalika kwa ulendo umenewu – pafupifupi makilomita 129/ulendo wa masiku anayi. Kodi kunali kovuta kotani kuyenda ulendo wautali ngati umenewu? (Kwa ana a Kalasi Yachiwiri muyenera kuonjezera kunena kuti chinali chikonzero cha Mulungu kuti mwanayo akabadwire ku Betelehemu!)</li><li>• Pamene anafika, mu mzindamo munali anthu ochuluka kwambiri ndipo sanathe kupeza malo oti agone. Nthawi iyi n’kuti mwana amene analonjezedwa ali pafupi kubadwa. Iwo anakagona m’mene munkakhala ziweto. <b>(Luka 2:6-7)</b></li><li>• Yesu atabadwa, anamukulunga mu nsalu ndi kumugoneka modyera ng’ombe kapena gome. <b>(Luka 2:6-7)</b> N’chifukwa chiyani Yesu anamukulunga mu nsalu zimenezi ndi kumugoneka modyera ng’ombe? Thandizani ana kuti amvetsetse kupambana kwa mwana ameneyu yemwe anabadwira malo onyozeka kwambiri. Siyanitsani kubadwa kwa mwana uyu ndi momwe ana amabadwira kudera kwanuko.</li><li>• Palibe Mwana wina anabadwa ngati Yesu. Iye ndi Mwana wa Mulungu. Iye analolera kuchoka Kumwamba ndi kudzabadwa pa dziko lapansi kuti atipulumutse ku machimo athu. <b>(Mateyu 1:21)</b></li><li>• Tiyenera kukumbukira kuti ili ndiye tanthauzo la Khrisimasi ndipo tikuyenera kuyamika Mulungu chifukwa cha chikondi chake potumizira Mpulumutsi.</li></ul> <p><b>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</b></p> <p><b>Kuonetsa:</b> Onani FBI pa Zoonjezera B – Kubadwa kwa Yesu.</p>
<b>PHUNZIRANI</b>	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <b>Luka 2:7.</b>
<b>KUMBUKIRANI</b>	<ul style="list-style-type: none"><li>• Kodi anali pa ubwenzi ndi Yosefe ndi ndani?</li><li>• Kodi Mariya ndi Yosefe ankakhala kuti?</li><li>• Kodi Yosefe ndi Mariya anayenda ulendo wopita kuti?</li><li>• N’chifukwa chiyani Yosefe ndi Mariya anali ku Betelehemu?</li><li>• N’chifukwa chiyani ankakhala m’mene ankasungamo ziweto?</li><li>• Kodi mwana Yesu anamugoneka muti?</li><li>• N’chiyani chimachititsa Yesu kukhala wapadera?</li><li>• N’chifukwa chiyani timafuna Mpulumutsi?</li></ul>

# Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

## Maphunziro a Kalasi Yoyamba

- Sabata lililonse pali mapeji anayi amene akufunika kuchekenira ndi kulembamo mawu pang'ono.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 amene akuyenera kuperekedwa kuchokera pa marikisi 80 a mwezi onse.
- Ana amene akuphunzira maphunziro a Kalasi Yoyamba iwo sakuyenera kuwerenga chifukwa sangathe kuwerenga bwino ndipo tikuyembekezera makolo/owang'anira/atsogoleri awo kuwathandiza.

## Maphunziro a Kalasi Yachiwiri

- M'buku muli maphunziro anayi pa sabata.
- M'phunziro lililonse muli nkhani. Ophunzira akuyenera kupeza mawu osiyanasiyana m'phunziro, ndi kuchekenira, kutsiriza Mavesi Oloweza ndi zina zambiri.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 pa marikisi 80 a mwezi uliwonse pamene atsiriza maphunziro onse molondola.

## FUNDO ZA KACHONGEDWE

### GUTANGA AMANOTA

Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:

- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolemba, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitso kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.

Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

## KALASI Yoyamba

### Ndemanga zina

“Chikondi – Ine ndasangalala kuti inu mwayamba maphunziro awa ndipo ndikukhulupirira kuti muwakonda. Zochekenira zanu ndazikonda. Kodi mumapita ku sukulu? Ndikuyembekezera kumva kuchokera kwa inu posachedwa”

“Wachita bwino, Andrey. Wachekenira bwino kwambiri! Kodi zimavuta pamene mumachekenira mizere ya m'kati? Inu musiyako zochepa zokha munachekenira pang'ono phunziro lapita lija.”

### Ndemanga zauzimu

“Wachita bwino, Sarah. Yairo analitu munthu wokondwa kwambiri pamene Yesu anamuthandiza.”

“Yankho labwino kwambiri! Nkhani ya kufa kwa Yesu ndi yomvetsa chisoni, koma chokondweretsa ndi chakuti lye anaukanso.”

## KALASI Yachiwiri

### Ndemanga zina

“Yankho labwino, Chimwemwe – Ine ndikukhulupirira kuti aphunzitsi ako akusangalala kwambiri ndi ntchito yako ku sukulu!”

“Ine ndikudziwa kuti posachedwapa ndi tsiku lako lobadwa, Chisomo. Kodi udzachita phwando? Udzachitira kuti? Udzakhale ndi tsiku lopambana kwambiri!”

“Iwe wayesetsa kwambiri. Pali zolakwika zochepa chabe. Usamayiwale kuonanso mayankho nthawi iliyonse.”

### Ndemanga zauzimu

“Ine ndasangalala ndi mmene wachekenira chithunzi cha Yesu ali nkhandu modyera ng'ombe. Kodi sizinali zabwino kuti Mulungu atumize Mwana wake ku dziko lapansi kwa ife?”

“Mitundu yako ndayikonda kwambiri! Zekariya anapereka dipo chifukwa cha kusankhulupirira zimene Mulungu ananena. Iye anakayikiranso Mawu a Mulungu.”

“Mayankho abwino kwambiri. Munthu amene anakumana ndi Filipo ku chipululu anapita kwawo akusangalala kwambiri. Iye anamva ndi kukhulupirira nkhanu yabwino ya Yesu.”

## Zoonjezera A - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A7	Petulo	<b>Petulo awuza anthu za Yesu</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-ascension/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-ascension/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-pentecost/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-pentecost/</a>
		<b>Petulo achiritsa munthu wolumala miyendo</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/lame-beggar-healed/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/lame-beggar-healed/</a>
		<b>Petulo m'ndende</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/</a>
		<b>Petulo amasulidwa</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/</a>
A8	Petulo	<b>Petulo athandiza Dorika</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-dorcas/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-dorcas/</a>
		<b>Mulungu aphunzitsa Petulo</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-cornelius/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-cornelius/</a>
		<b>Petulo ndi Korneliyo</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-cornelius/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-cornelius/</a>
		<b>Petulo apulumutsidwa</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-peter-prison/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-peter-prison/</a>
A9	Yakobo	<b>Yakobo anamiza m'bale wake</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-jacob-esau/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-jacob-esau/</a>
		<b>Yakobo anamiza abambo ake</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-jacob-isaac/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-jacob-isaac/</a>
		<b>Yakobo akumana ndi Mulungu</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-jacob-ladder/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-jacob-ladder/</a>
		<b>Yakobo apeza mkazi</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-jacob-ladder/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-jacob-ladder/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-isaac-wife/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-isaac-wife/</a>



## Zoonjezera B - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zinthunzi Zaulelele m’Baibulo

	Mutu	Nkhani m’Chithunzi
A10	Akhristu Oyambirira	<b>Stefano apedwa chifukwa cha Yesu</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/stephen-martyred/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/stephen-martyred/</a>
		<b>Filipo afalitsa uthenga wabwino</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/isc-objects/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/isc-objects/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/philip-ethiopian/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/philip-ethiopian/</a>
		<b>Saulo ndi kuwala kwakukulu</b>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-saul-damascus/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-saul-damascus/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-paul-damascus/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-paul-damascus/</a>
		<b>Kusinthika kwa Saulo</b>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-saul-damascus/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-saul-damascus/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-paul-damascus/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-paul-damascus/</a>
A11	Paulo	<b>Paulo (Saulo) ku Antiokeya</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-cyprus/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-cyprus/</a>
		<b>Paulo (Saulo) ku Kupro</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-cyprus/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-cyprus/</a>
		<b>Paulo akumana ndi Lidiya</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-earthquake/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-earthquake/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-antioch-philippi/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-antioch-philippi/</a>
		<b>Paulo ndi Sila m’ndende</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-earthquake/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-earthquake/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-paul-prison/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-paul-prison/</a>
A12	Nkhani ya Khrisimasi	<b>Zakariya ndi Elizabeti</b>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-zechariah/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-zechariah/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-zacharias/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-zacharias/</a>
		<b>Mariya ndi Gabrieli</b>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-mary-angel/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-mary-angel/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-zacharias-elizabeth/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-zacharias-elizabeth/</a>
		<b>Kubadwa kwa Yohane</b>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-zechariah/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-zechariah/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-zacharias-elizabeth/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-zacharias-elizabeth/</a>
		<b>Kubadwa kwa Yesu</b>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-jesus-born/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/lis-jesus-born/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/birth-jesus-preschool/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/birth-jesus-preschool/</a>

## Zoonjezera A - Kalasi Yachiwiri Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A7	<b>Petulo</b>	<b>Petulo alalikira</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-12-e/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-12-e/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-ascension/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-ascension/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/pentecost/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/pentecost/</a>
		<b>Petulo achiritsa munthu wolumala miyendo</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/lame-beggar-healed/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/lame-beggar-healed/</a>
		<b>Petulo m'ndende</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/</a>
		<b>Petulo atulutsidwa m'ndende</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-john-arrested/</a>
A8	<b>Petulo</b>	<b>Petulo athandiza Dorika</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-dorcas/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-dorcas/</a>
		<b>Petulo aona masomphenya</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-cornelius/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-cornelius/</a>
		<b>Petulo ndi Korneliyo</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-cornelius/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-cornelius/</a>
		<b>Petulo m'ndende (kachiwiri)</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-prison/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/peter-prison/</a>
A9	<b>Yakobo</b>	<b>Yakobo anamiza m'bale wake</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/esau-jacob/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/esau-jacob/</a>
		<b>Yakobo anamiza abambo ake</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-deceives/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-deceives/</a>
		<b>Yakobo akumana ndi Mulungu</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-dream/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-dream/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/isc-objects/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/isc-objects/</a>
		<b>Yakobo apeza mkazi</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-wedding/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-wedding/</a>

## Zoonjezera B - Kalasi Yachiwiri Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A10	Akhristu Oyambirira	<b>Stefano apedwa chifukwa cha Ambuye</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/stephen-martyred/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/stephen-martyred/</a>
		<b>Filipo afalitsa uthenga wabwino</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/philip-ethiopian/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/philip-ethiopian/</a>
		<b>Saulo aona kuwala kwakukulu</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-conversion/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-conversion/</a>
		<b>Kusandulika mtima kwa Saulo</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-conversion/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-conversion/</a>
A11	Paulo	<b>Paulo (Saulo) ku Antiokeya</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-cyprus/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-cyprus/</a>
		<b>Paulo (Saulo) ku Kupro</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-cyprus/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-cyprus/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-cyprus/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-cyprus/</a>
		<b>Paulo akumana ndi Lidiya</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-antioch-philippi/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-antioch-philippi/</a>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-earthquake/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-earthquake/</a>
		<b>Paulo ndi Sila m'ndende</b>
		<a href="http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-earthquake/">http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-paul-earthquake/</a>
A12	Nkhani ya Khrisimasi	<b>Zakariya ndi Elizabeti</b>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/zechariah-elizabeth/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/zechariah-elizabeth/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-002-zechariah/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-002-zechariah/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-zacharias/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-zacharias/</a>
		<b>Mariya ndi mngelo Gabrieli</b>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-jesus-birth/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-jesus-birth/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-003-birth-announcement/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-003-birth-announcement/</a>
		<b>Kubadwa kwa Yohane</b>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/zechariah-elizabeth/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/zechariah-elizabeth/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-005-birth-john/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-005-birth-john/</a>
		<b>Kubadwa kwa Yesu</b>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-jesus-birth/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-jesus-birth/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-007-birth-jesus/">https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-007-birth-jesus/</a>
		<a href="https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-birth/">https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-birth/</a>



© Bible Educational Services 2020

[www.besweb.com](http://www.besweb.com)

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 02/2023  
(Chichewa)